

Liwu La Chizindikiro
Denham Springs, Louisiana, USA
Malichi 21, 1964

1 Mukhale chiimire kwa mphindi pang'ono chabe Pamaso pa Ambuye. Tiyeni ife tiwerenge kuchokera mu Mawu

Ake, mu Eksodo, mutu wa 4.

...Mose anayankha ndipo anati, Koma, taonani, iwo sakandikhulupirira ine, kapena kumvera mawu anga: pakuti iwo adzati, YEHOVA sanawonekere kwa iwe.

Ndipo YEHOVA ananena naye iye, Icho ndi chiyani chiri mdzanja lako?...iye anati, Ndodo.

Ndipo iye anati, Iponyere iyo pansi. Ndipo iye anaiponyera iyo pansi, ndipo iyo inasanduka njoka; ndipo Mose anaithawa iyo.

Ndipo YEHOVA anati kwa Mose, Tambasula dzanja lako, nuigwire iyo kumchira. Ndipo iye anatambasula dzanja lake, ndipo anaigwira iyo, ndipo iyo inasanduka ndodo mdzanja lake:

Kuti iwo akakhulupirire kuti YEHOVA Mulungu wa makolo awo, Mulungu wa Abrahamu, Mulungu wa Isaki, ndi Mulungu wa Yakobo, wawonekera kwa iwe.

Ndipo YEHOVA ananenanso mopitirira ndi iye, Ika tsopano dzanja lako mchifuwa. Ndipo iye anaika dzanja lake mu chifuwa chake: ndipo pamene iye analiturutsa ilo, taonani, ilo linali lakhate ngati chisanu.

Ndipo iye anati, Bwezeranso dzanja lako mchifuwa chako. Ndipo iye anabwezeranso dzanja lake mchifuwa chake kachiwiri; ndipo analichotsanso ilo mu chifuwa chake, ndipo, taonani, ilo linasandulikanso kachiwiri monga thupi lake linalo.

Ndipo zidzafika pochitika kuti, ngati iwo sakakukhulupirira iwe, ngakhale kumvetsera kwa liwu la chizindikiro choyamba, kuti iwo adzakhulupirira liwu la chizindikiro chotsatilachi.

Ndipo zidzafika pochitika kuti, ngati iwo sakakukhulupirira iwe, zizindikiro ziwiri izi, ngakhalenso kumvetsera kwa liwu lako, kuti iwe ukatunge madzi a ku mtsinje, ndipo ukawatsanulire iwo pa nthaka youma: ndipo madzi amene iwe wawatunga kuchokera ku mtsinje adzasanduka mwazi pa...nthaka youma.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu kwa pemphero. Tsopano kodi inu muli ndi chopempha, madzulo ano, chimene inu mukufuna kuti muwadziwitse Ambuye, ingokwezerani mmwamba manja anu ndikuti, "Ambuye, mundikumbukire ine tsopano. Ine ndiri nacho chosowa."

Atate athu Akumwamba, ife tikukuyandikirani Inu kachiwiri madzulo ano, pozindikira kuti pamene ife tikuweramitsa mitu yathu ku nthaka kumene ife tinachokerako, ndipo, ngati Inu muchedwa, ife tidzabwereranso ku nthaka. Koma ndi chiyembekezo chodala cha lonjezo chimene chiri mwa Khristu, kuti onse amene ali mwa Mulungu Khristu adzawabweretsa limodzi ndi Iye. Ife—ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha lonjezo laulemerero ili. Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mukumbukire mmodzi aliyense wa iwo amene anakweza mmwamba manja awo, langanso, Ambuye.

Ine ndikupemphera, usikuuno, kuti mu kutsekera kwa ora ili la chikhulupiriro, kuti Inu muwapatse anthu chikhulupiriro chotero usikuuno, kuti Ambuye Yesu adzakhale weniweni kwambiri kwa mmodzi aliyense wa ife, kuti pasakhale munthu wofooka pakati pathu ukatha usikuuno. Mulole wochimwa aliyense akazindikire kuti iye ali mu Kukhalapo kwa Ambuye Yesu, ndiyeno akalape machimo ake, ndi kupereka mtima wake kwa Inu, ndi kudzazidwa ndi Mzimu; mu maora oyipa otsiriza awa, pamene ife tikuziwona izo ngati mthunzi wawukulu ukukwawira pa dziko lapansi.

Ife tikupempherera, Mulungu, utsogoleri Waumulungu, usikuuno, kwa olankhula ndiponso kwa omvetsera. Mulole Mzimu Woyera utenge msonkhanowu tsopano ndipo munyemere Mkate wa Moyo kwa mmodzi aliyense wa ife monga mwakusowa kwathu, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake. Amen.

Mukhoza kukhala.

2 Ine ndikudalira kuti usikuuno ife tikhoza kukwaniritsa chimene ife tikuyesera kuti anthu achiwone, che—chenicheni chake cha kukhala ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.

Tsopano, mawa madzulo hafu pasiti thuu, onse amene ali ndi makadi a pemphero adzakhala akupemphereredwa. Ndiyeno pofuna kukhala otsimikiza kuti palibe amene wasiyidwa, wopanda makadi a pemphero, usiku uliwonse ife tikumapereka makadi ena a pemphero. Ndipo iye adzawaperekanso iwo mawa, pafupi...Ine ndikuganiza, pafupi hafu pasiti wani kapena chinachake monga choncho, basi msonkhanowo usanayambike. Ndipo onse amene akufuna kuti adzapemphereredwe, aliyense wa okonedwa anu, aloleni iwo adzabwere ndipo adzatenge khadi la pemphero. Iwo ndithudi adzakhala o—olandiridwa kwa khadi la pemphero. Ndipo ife tikuti...

3 Ine ndiwapempherera anthu, poyika manja pa iwo ndi kuwapempherera iwo. Tsopano ngati chikhulupiriro chanu sichingakwere kufika mu Kukhalapo kwa Ambuye Yesu ndi kumulandira Iye ngati mchiritsi wanu, ndipo inu ndikukhulupirira kuti ngati ife tingapemphere ndi kuyika manja pa inu, kuti izo zikuthandizani, chabwino, ife ndithudi tiri pano kuti tichite chirichonse chimene inu mukuchikhumba.

Ndi chifukwa chake ine ndinazisiya izo mpaka mochedwa, ndinatalikitsa, ndinawona kuti aliyense amene ine ndikanatha, kuti adzakhoze kufikira ndi kumugwira Mulungu pa maziko amenewo. Ndipo ife tiribe ochuluka kwambiri. Alipo... Chipindachi si chachikulu, ndipo kotero ife tiribe anthu ochuluka kwambiri. Ndipo ife tikhoza kudzatenga mawa madzulo ndi kudzapempherera onse amene ife tiri nawo kuno, kuwaika madzulo kwa cholinga chimenecho, kuti tidzapempherere odwala.

Ndipo ife tiri pano kuti tidzachite chirichonse chimene ife tingathe kuti tithandizire kuupanga moyo kukhala wabwinoko kwa inu, kudzakupuzani zolemetsazo, mu ulendo uwu umene ife tiri kuyendamo.

Ndiyeno pa nthawi iliyonse, imene aliyense angamverere kuti—kuti iwo akufuna kuti abwere kwa Ambuye Yesu, ziribe kanthu kuti ndi gawo lanji la msonkhano limene likuchitika, inu muzibwerabe ndiye. Musadzadikirire mpaka akamapanga kuitanira paguwa. Musadzadikirire mpaka mupatsidwe kuitanidwa. Inu mudzangobwera pomwepo, mudzambulandire Khristu, ndi kubwera pomwepo ndi kudzamuvomereza Iye pomwepo. Pakuti ndicho cholinga chathu chenicheni chokhalira pano, ndi kuti tiziwona miyoyo ikubadwira mu Ufumu wa Mulungu.

4 Ndipo tsopano, mawa ndi Lamlungu, ndipo tidzakhala ndi Sande sukulu, mipingo. Chifukwa chimene ife tikumakhalira ndi misonkhano yathu madzulo, Lamlungu, ndikuti ife tisasokoneze msonkhano uliwonse nkomwe. Ife timakhulupirira kuti Mkhristu aliyense amayenera kuti azikhala ndi—tchalitchi cha kwawo kumene iwo amapitako. Mkhristu aliyense amayenera kuti azikomana penapake ndi okhulupirira. Ndipo kulikonse kumene inu mumakomana, chimenecho ndicho tchalitchi.

Tsopano, ngati ine ndikanamakhala kuno, ine ndikanakhala wa mmodzi wa mipingo iyi kuno, imene azibusa awa kuno, amene tikuchita nawo, akuyimira. Bwanji? Chifukwa iwo ali pano akhala pa nsanja, kuti awonedwe ndi anthu onse, kuti iwo akugwirizana nazo zimene zikuchitikazi. Iwo akukhulupirira mu mtundu uwu wa utumiki, machiritso Auzimu, Ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi zina zotero. Iwo ali pano kudzachitira umboni kwa zimenezo. Iwowo ndi amene anandiitana ine kuti ndibwere kuno, kuti mwina utumiki umene Ambuye wandipatsa ine ukhoza kuthandizira gulu lawo.

Tsopano ameneyo ndiye m'busa weniweni, amene amafunafuna zopindulitsa zauzimu zonse zimene iye angathe, za chirichonse chimene Mulungu akuchita, amene akuyesetsa mwakukhoza kwake kuti awuthandizire mpingo wake kuti ukasunthire mtsogolo kwa Mulungu. Ine ndithudi ndimavula chipewa changa poyamikira m'busa woteroyo.

Ndipo amuna awa amachita zimenezo movutikira, nawonso. Inu mukhoza kukhulupirira zimenezo kuti ndi zoono. Iwo amachita zimenezo movutikira. Ndipo ine—ine ndithudi ndikuyamikira chifukwa cha munthu wopambana chotero wa Mulungu, amene amalolera kuti atenge malo awo ndi malo awo antchito monga mmene iwowo akumvererera, ndi—kukakhulupirira. Mulungu aziwadalitsa iwo nthawizonse!

5 Ndipo ndine wotsimikiza kuti iwo akakuchitirani inu zabwino. Tsopano, ngati ndinu mlendo pano, mukafufuze kumene abale awa ali ndi mipingo yawo, kumene iwo amakhalako. Mukawachezere iwo mawa. Iwo adzakakhala ndi misonkhano yapadera, ndipo pali atumiki pano amene akakhale akulankhula ku matchalitchi osiyanasiyana, ndipo monga zalengezedwa. Chotero mukakhale nawo pa iyo mawa.

Ndiyeno mawa madzulo, ngati inu mukufuna kuti mudzabwere ku msonkhano wotsekera, ife ndithudi tidzakhala okondwa kudzakhala nanu inu. Mipingo yonse, zipembedzo zonse, ndi za aliyense. Aliyense ndi wolandiridwa; Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Apentekoste, a mpingo wa Khristu, mpingo wa Mulungu, Akatolika, Myuda wachi Orthodox, wachikunja, chirichonse chimene inu muli. Ndife...Ndinu olandilidwa.

“Inu mukuti, 'Wachikunja'?” Inde, bwana.

Ngati wachikunja angabwere mu msonkhano ndi kudzakhala pansu ndi kukhala wakhalidwe, iye ndi wolandiridwa basi ngati wina aliyense. Kulondola. Chinachake, ndi chimene ife tikumufunira iye pano, kuti chinachake chikhoza kuchitidwa chimene chingathe kumuthandizira iye kuti akawone kulakwitsa kwake, ndi kubwera kwa Ambuye. Pakuti ife...Ndithudi.

6 Ndi angati anayamba awerengapo masomphenya aang'ono amene magazini ya Christian Business Men inasindikiza, ndipo ine ndikukhulupirira magazini pang'ono enanso-...za, Kuyang'ana Kudutsa Katani La Nthawi? Tsopano zimenezo ndi zoono, mzanga. Inu simungakwanitse kuti muphonye zimenezo. Ine—ine ndakhala ndiri munthu wosiyana kuchokera pamene. Ine ndikudziwa kuti izo ndi zenizeni, chotero ine—ine—ine ndikungodalira kuti palibe aliyense wa inu adzakaphonye Kumwamba kwakukulu uko kumene Mulungu wawakonzera okhulupirira. Ngati inu mudzatero, kodi inu mwapindula chiyani pa dziko lapansi lino? Chifukwa, inu simukudziwa kuti mudzachoka liti pa dziko lino. Koma inu mukudziwa chinthu chimodzi,

inu ndithudi mudzayenera kuti mudzalisiye ilo. Kotero ngati izo ziri zoon, ndiye ife sitingakhale opusa kwambiri kuti tiziyesera kuti—kuti titenge basi monga...Ife sitingakwanitse kuti titenge mwayi wa mtundu uliwonse. Mukuona, musingokumbukira, muzikhulupirira Mawu a Mulungu ndi lonjezo lirilonse la Iwo.

7 Tangoganizani, ndi chiani chinayambitsa matenda onsewa, kupweteka kwa mutu konseku, imfa iliyonse, vuto lirilonse, chisoni chonsechi, mwana wamng'ono wolumala uyu, zinthu zonse izi, kulumala, khungu, chipatala chirichonse kuti chikamangidwe? Chifukwa munthu mmodzi sanakhulupirire basi gawo limodzi laling'ono la Mawu. Ameneyo anali Eva. Satana anangowakutira iwo kwa iye. Osati kuwawerenga mobwereza, koma anawakutira iwo kwa iye, anati, "Ndithudi...Ambuye ndi wabwino kwambiri."

Inu mumamva zambiri lero zakuti, Mulungu ndi Mulungu wabwino. Iyeyo ndi Mulungu wabwino, koma kumbukirani Iye ndi Mulungu wachiyero, Mulungu amene sangalilambalale tchimo. Chilango chinalipiridwa, ndipo inu muyenera kuzilandira izo pa maziko Ake. Ndipo kumbukirani, Iyeyo ndi Mulungu wokwiya, Mulungu wamkwiyo. Ndipo inu mudzakaima pamaso pa Mulungu wokwiya, osati kokha Mulungu wa zabwino ndi chifundo. Usikuuno Iyeyo ndi Mpulumutsi wanu; Tsiku limenelo Iyeyo adzakakhala Woweruza wanu.

Chotero muzikhala wotsimikiza kuti iwe usasiye chinthu chimodzi chosachichita, mzanga. Izo—izo sizidza... Izo sizidzakuthandizani. Musamati—musamapite pa izo mwachisawawa. Muzikhala otsimikiza, muzitsimikizira mowirikiza, chifukwa inu simudzapezanso mwayi wina. Uwu ndi mwayi wanu wokhawo, pamene inu mudakali pano pa dziko lapansi.

8 Kumbukirani mnyamata mwini chuma ndi Lazaro, panali phompho lalikulu pakati pa iwe ndi Iye, limene panalibe munthu anayamba wawolokapo, kapena adzawoloke nkomwe. Mukuona? Pamene inu—pamene inu mufa, izo zimathera pomwepo. Ine ndikudziwa anthu amadzinenera kuti iwo amakupempherera iwe kuti uchokeko ku malo amenewo, koma inu musadzazikhulupirire konse zimenezo. Zimenezo ndi zosiyana ndi Mawu a Mulungu. Mukuona? "Komwe mtengo umatsamira, ndi kumene iwowo umakagwera." Ndipo Yesu anati, Mwiniwake, anati, "Pali phompho, lakuti, pamene munthu afa ndipo napita ku gehena, iye samatha (sangathe konse) kubwera Kumwamba. Palibe munthu amene anayamba waliwolokapo ilo, ndipo sadzakhalapo konse." Izo zikukhazikitsa zimenezo, monga momwe ine ndikudziwira. Pamene Yesu ananena kuti izo zinali momwemo, zimenezo zinali zonse za izo.

Kotero ingokumbukirani, ndi mwayi wanu pakali pano, ndipo usikuuno ukhoza kukhala mwayi wanu wotsiriza.

9 Kodi inu mungakhoze konse kuzimvetsa zimene zikuchitikazi? Ngati inu mungathe kungoziwona izo! Ine ndikuyembekeza kuti inu simukuganiza kuti kulankhula monga choncho, kuti ine ndikuyesera kuti ndikukopereni inu kuti muziyang'ana pa munthu wina, kapena kumukhulupirira munthu wina. Ine sindikuchita zimenezo, mzanga. Ine ndikuyesera kuti ndikufikitseni inu pokhulupirira Yemwe iye ali amene ife tiri Pamaso pake tsopano. Yesu Khristu, Mulungu kumene amene ati adzakuweruzeni inu pa Tsiku limenelo, ali pano akuzizindikiritsa Yekha pakati panu, chinthu kumene chimene Iye analonjeza kuti Iye adzachichita mu masiku otsiriza ano.

Ine ndikuganiza M'bale Price, mmawa uno pa kadzutsa, anapereka kulosongosola kwabwino kotero kwa kubwera pa ngodya, ndiye ndi kukhota ngodyayo. Kodi inu zinakukomerani zimene zija? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Ndithudi zinatero. Izo zinali, zinaikidwa mwabwino kwambiri.

10 Tsopano, kotero takumbukirani, nthawizina pangodya, koma tiyeni tizikumbukira ife timayenera tizikhota ngodya zimenezi. Ine ndinalalikirapo pa izo, nthawi ina, ndipo ndinadzitcha izo, Mphambano. Ife timafika pa mphambano, kawirikawiri, ife timayenera kuti tipite njira iyi ndi kuzungulira njira zosiyanasiyana.

Tsopano usikuuno, kwa maminiti pang'ono otsatirawa, ine ndikufuna kuti nditenge phunziro la—la: Liwu La Chizindikiro. Ndipo tsopano chochitika chathu chikutsegukira, usikuuno, mu Bukhu la Eksodo, ndipo eksodo amathanthauza "kukhala mukutuluka; kutulutsidwa." Tsopano muyesetse kuti mumvetsere mwatcheru momwe inu mungathere.

Ine ndikufuna kuti ndidzalalike kwa inu nthawi inayake, ndinu omvetsera abwino kwambiri, koma zangokhala kuti ine ndiribe mawuwo. Basi ndine womangika pang'ono pa zimenezo, ndipo ine ndikudziwa chimene icho chidzakhale. Ine ndiyenera kuti ndipume pang'ono tsopano, kwa pafupi masiku eyiti kapena teni, ine ndisanayambe msonkhano wotsatira. Mukuona, si msonkhano umodzi wokha uwu kuno. Ndi msonkhano, watsiku ndi tsiku, sabata ndi sabata, mwezi ndi mwezi, chaka ndi chaka, mukuona, ndipo inu mukhoza kulingalira.

Ndipo ndikaganiza za nthawi zonsezi, chaka ndi chaka, palibe nthawi imodzi imene Iye anayamba wanenapo chirichonse koma chimene chakhala chiri changwiro, ndendende choonadi; mu zinenero zonse, kuzungulira pa dziko lapansi lonse, nthawi zisanu ndi ziwiri. Mukuona? Palibe munthu, kulikonseko, amene anganene kalikonse koma kuti zonse zakhala mwangwiro, ndendende pa dontho, nthawi zonse. Pamene

Iye anena kuti chinthu chinachake chichitika, icho chimadzachitika ndendende mwanjira imeneyo. Kuzinena izo kwa masabata ndi miyezi, ndi zaka, ngakhalenso, izo zisanachitike, ndipo nthawizonse izo zimadzakhala ndendende pa dontho. Palibe nthawi iliyonse zinayamba zalepherapo, ndipo izo sizidzatero konse, chifukwa ameneyo ndi Mulungu. Tsopano, ine ndikhoza kulephera, ngati munthu. Musamandiyang'ane ine ngati chitsanzo chanu, chifukwa ine—ine ndiri chimodzimidzi ngati inu, wochimwa basi wopulumutsidwa mwa chisomo. Koma ameneyo ndi Mulungu, chauzimucho, mwaona, akuzidzindikiritsa Yekha. Iye sakusowa kuti azichita izo, koma Iye analonjeza kuti Iye azidzachita zimenezo.

11 Yesu ankachiritsa chifukwa chakuti izo zimakwaniritsa Mawu. Iye ankachita zinthu zimenezo chifukwa chakuti Mawu a Mulungu amakwaniritsidwa.

Ndi chifukwa chimene Iye akuchitira izo lero, kuti Mawu akakhoze kukwaniritsidwa, zimenezo ine ndaziwerenga mobwereza kwa inu, usiku ndi usiku.

Tsopano zindikirani ndiye pamene Kukhalapo Kwake kukakhala pafupi, Iko, ndithudi Iko kumabweretsa kutengeka. Monga ine ndimanenera mmawa uja, “Chirichonse chopanda kutengeka ndi chakufa.” Ndipo chipembedzo chirichonse chimene chiribe kutengeka kwina kwa icho, inu kuli bwino mukachikwirire icho, icho ndi chakufa. Iko kumabweretsa kutengeka. Iye amatifulumizitsa ife. Koma pamene ife tafulumizitsidwa, tiyeni tikumbukire ndi Chiyani chatifulumizitsa ife. Ndi chiani chinachita izo? Ndi Kukhalapo kwa Mzimu Woyera, Yesu Khristu pakati pathu, kudzisonyeza Yekha kuti Iye ali wamoyo. Osati thupi logwirika; pamene nthawi imeneyo, pamene thupi logwirikalo lidzabwere kuchokera Kumwamba, nthawi siidzakhapanso. Ndizo zonse za izo. Ndipo ife tikudziwa kuti ife tiri mmenemo, tikukhala moyo mu masiku otsiriza, pamene zinthu izi ziti zidzachitike.

Tsopano, Mulungu anayamba wakhalapo nako kutuluka.

Pali...

12 Chirichonse chimayenda mu zitatu, ndi Mulungu. Mulungu amakhala wangwiro mu zitatu. Kubwera koyamba kwa Khristu, kuti adzamuwombole Mkwatibwi Wake; kubwera kwachiwiri kwa Khristu, kuti adzamalundire Mkwatibwi Wake; kubwera kwachitatu kwa Khristu, ali ndi Mkwatibwi Wake, kuti adzalamulire mu Zakachikwi. Chirichonse chikuyenda mu zitatu.

Tsopano, pakhala pali, padzakhala, kutuluka kutatu. Kumodzi kwa iko, Mulungu anawabweretsa iwo mu chombo, kuti atuluke, anayenda pamwamba pa dziko lapansi. Nthawi yotsatira, Mulungu anawabweretsa iwo kuti atuluke ku—ku Igupto. Ndipo nthawi yotsatira, Mulungu akuwatengera iwo mmwamba. Kulowa, kutuluka, kukwera mmwamba! Eksodo wotsatira kudzakhala kukwera mmwamba. Iye tikuyang'anizana nako kumodzi tsopano, nthawi yopita- mmwamba.

13 Ndendende monga momwe moyo umachitira chinthu chomwecho. Iye timabwera mkati mu moyo, ife tidzatuluka kunjira kwa moyo, tidzaukira mmwamba kupita ku moyo, ndendende basi chinthu chomwecho. Kotero ndife...

14 Chochitika chathu chikutsegukira usikuuno ku eksodo, ndipo Mulungu anali akukonzekera kuti alitenge fuko Lake. Israeli ndi fuko. Mulungu samachita naye Israeli ngati munthu payekha. Israeli ndi fuko, nthawizonse ankachita nawo iwo. Ndipo mu masiku otsiriza, pambuyo pa—pakuti mpingo wapita, ndiye Mulungu adzapulumutsa Israeli ngati fuko. Iye ali ku dziko la kwawo tsopano, akukonzekera zimenezo. Ndipo iwo adzapulumutsidwa, Baibulo limati, “Fuko lidzabadwa mu tsiku limodzi.” Mulungu samachita ndi Ayuda ngati munthu mmodzi payekha. Iye amachita nawo iwo ngati fuko, Israeli, nthawizonse, chifukwa ilo ndi fuko Lake. Ndipo apa Iye akukonzekera kuti alibweretse fuko lake lituluke mu fuko, mu eksodo, kuwabweretsa anthu Ake kuwachotsa ku chiweruzo.

15 Ndipo madzi omwewo amene anamiza nawo dziko lapansi, anamupulutsa Nowa. Mukuona? Ndipo Mzimu Woyera womwewo, umene anthu akuwukana lero, udzawulandira Mpingo ndi kudzawutengera Iwo mmwamba, ndi kudzabweretsa chiweruzo pa osawukhulupirira Iwo. Yesu anatero.

Pamene iwo anamutcha Iye, “Belezebule,” mwakulankhula kwina, “Iye anali wambwebwe.” Iwo...

Iye anati, “Ine ndikukhululukirani inu chifukwa cha zimenezo,” Mwana wa munthu. Nsembe inali isanapangidwe. “Koma pamene Mzimu Woyera udzabwera mukadzachita chinthu chomwecho, mawu amodzi kuwutsutsa Iwo simudzakhululukidwa konse mu dziko lino ngakhale mdziko liri nkudza.” Iwo uyenera kuti ukanidwe, ndiyeno chiweruzo chidzakantha zikadzachitika zimenezo. Mukuona, vuto lake ndi lakuti ife...

16 Zikundikumbutsa ine za nthawi ina nkhani imene ine ndinawerenga, ya woyenda panyanja wakale akuchokera ku nyanja, ndipo—wandakatulo wa Chingerezi anali akupita ku nyanja. Ndipo kotero wandakatuloyo anali atalemba zochuluka za nyanja, koma iye anali asanaiwonepo iyo, kotero iye anali ali akuyenda wa kumeneko. Ndipo mmalinyero wachikulireyo anati kwa iye, ali ndi kaliwo wake mkamwa

mwake, anati, "Iwe ukupita kuti, munthu wanga wabwino?"

Iye anati, "Ine ndikutsikira ku nyanja uko." Iye anati, "Ine sindinayambe ndaiwonapo iyo. Ine ndakhala ndikulemba za iyo, ndi zomwe ena amanena, koma," anati, "o, ndine wokondowezeka kwambiri podziwa kuti ndikuyandikira ku nyanja." Iye anati, "O, kukanunkhiza madzi ake a mchere! Kukawona, mafunde ake aakulu oyera akugawanizikana pamwamba pake, ndi mlengalenga mobiliwira mukuzinyezimiritsa mokha, ndi kukazimva mbalame za kauye zikuwuluka pamwamba pake, o, ine ndikukondowezeka nalo lingaliro la kukaiwona iyo!"

Malinyero wachikulireyo anati, "Ine ndinabadwira kumeneko, zaka sikisite zapitazo, ine sindimawona kanthu kokongola kwambiri za iyo." Mwaona, iye anali atawona zochuluka kwambiri za iyo mpaka iyo inali yawamba kwa iye.

Tsopano ndiro limene liri vuto ndi mpingo wa Chipentekoste lero. Iwo wawona zochuluka kwambiri za Mulungu, mpaka Mulungu wakhala chozowereka kwa iwo. Musadzalole nkomwe kuti izo zidzachite zimenezol!

17 Kuno osati kale litali, mu Louisville, Kentucky. Kumene ine ndimachokerako, Jeffersonville, Indiana, ndi kuwoloka mtsinje kuchokera kumeneko. Dona anali akuyenda mu sitolo ya teni-senti. Ndipo iye (anali) anali ndi mnyamata wamng'ono pa mkono wake, ndipo iye amapita ku makauntala ndi kumakachita mwamanjenje. Iye amakhoza kunyamula chinachake, nkuchisonyeza icho kwa mnyamata wamng'onoyo; iye amangokhala ndi kumangoyang'ana. Iye akapita pa kauntala ina, ndi kukatola chinachake ndi kumusonyeza mnyamata wamng'onoyo; iye amangoyang'ana. Ndipo patapita kanthawi, iye ananyamula kabelu kakang'ono ndipo anayamba kukaliza iko, ndipo mnyamata wamng'onoyo anangoyang'ana. Ndipo iye anayamba kumalira, ndipo anaponyera manja ake mmwamba. Ndipo anthu mu sitolo ya teni-senti iyo anali akumuyang'ana iye, kotero iwo anapita kwa iye kuti akamufunse vuto lake.

Iye anati, "Ine ndiri ndi...Mnyamata wanga wamng'ono," anati, "iye ndi wa wasinkhu wa zaka zitanu zokha." Ndipo anati, "Ine...Mwadzidzidzi, pafupi chaka chapitacho, iye akatenga amangokhala ndi kumangoyang'ana tong'o." Ndipo anati, "I—ine ndinamutengera iye kwa adokotala," ndipo anati, "ndipo adokotala anamupatsa mankhwala enaake ndi zinthu." Ndipo anati, "Ndipo adokotala anandiuza ine, lero, kuti iwo akuganiza kuti iye ali bwino. Koma," anati, "iye sali bwino." Anati, "ine ndamugwedezera chirichonse pamaso pake, chimene chikanayenera kuti chikope tcheru cha mnyamata wamng'ono wa usinkhu wake. Chirichonse chimene chikanati chimukope mnyamata wamng'ono wa usinkhu wake, ine ndachigwedezera icho pamaso pake, ndipo iye akumangokhala ndi kumangoyang'ana tong'o." Anati, "Iye sali bwinobe."

Chimenecho ndi chinachake chonga mpingo wa Chipentekoste. Mulungu wagwedezera mphatso iliyonse, ili mu Baibulo, pamaso pawo, ndipo iwo akungokhala ndi kumayang'ana tong'o, ngati kuti ndi chinachake cholakwika. Yafika nthawi yoti tidzuke, amzanga, nthawi isanathe. Kumbukirani, Mulungu samagwedezera mphatso zimenezol kupatula ngati Iye akuyesera kuti akope tcheru chanu.

Mulungu anali akubweretsa fuko kuchokera mu fuko.

18 Chimodzimidzi monga Iye akuchitira tsopano, amubweretsa Mkwatibwi kuchokera mu mpingo, adzasiya wotsalira wa mbewu ya mkazi. Osankhidwa abweretsedwa kuchokera mu mpingo. Mpingo wa thupi utsala kuno kuti udzadutse mu chisautso. Osankhidwa amenewo nthawi zina amatchedwa "opatulidwa, osankhidwa, wotsalira."

Tiyeni tiwone momwe Iye anachitira izo pamenepo, chifukwa Iye samasintha nkomwe njira Yake yochitira zinthu. Mulungu ali nayo njira imodzi yochitira zinthu, ndipo ndi momwe Iye amachitira izo, ndipo ndiyo njira yolondola, nthawizonse. Muwone momwe Iye anachitira izo, ndi machitidwe omwe Iye anachitira izo, ndiyeno ife tikhoza kuziwona izi tsopano.

19 Ndine wofanizitsa zinthu, ndithudi. Ine ndiribe maphunziro. Ine ndimachita kuyang'ana mmbuyo ndi kukawona zimene Iye anachita. Ndipo ife timaphunzitsidwa kuti, "Chipangano Chakale chinali mthunzi wa zinthu zimene ziri nkudza." Kotero ngati ine nditayang'ana kuno ndipo sindinayambe ndaliwonapo dzanja langa, ndipo ine ndikuwona mthunzi wa dzanja langa, ndipo ine ndinali ndi zala zisanu, ine ndingakhale nalo lingaliro labwino kuti dzanja langa likafika pamenepo, ndikhala ndi zala zisanu. Kotero zimene nzikachitika kwa iwo zinali zitsanzo za momwe Mulungu amachitira zinthu, momwe Iye akuchitira izo tsopano.

Ndipo momwe Iye amachitira izo, Iye samasintha nkomwe kwa icho. Nthawi iliyonse, kudutsa mu Baibulo, Iye samasintha konse njira Yake yochitira zinthu. Mopitirira chimodzimidzi, chifukwa njira Yake yoyamba yomwe anachitira izo ndiyo njira yangwiro. Chifukwa, Iye sakadakhala ndi njira inayake, chifukwa Iye ndi wangwiro, ndipo, Iye, njira Zake zonse ndi zangwiro. Taonani momwe Iye anachitira izo.

20 Mose anaitanidwa ndipo anadzozedweratu kuti adzatenge ntchito iyi imene iye anali, iye anali—iye anali ataitenga. Mulungu...

Tsopano, ine ndikuganiza, ngati inu mungandikhululukire izo...Ine sindikunena izi mopupulumu. Ine ndikungonena, pa nsanja ino, i—ine sindikudziwa kanthu ndipo sindikufuna kudziwa kalikonse koma Mulungu. Tsopano, ine ndikuganiza kuti apo ndi pamene abale athu a Mvula Yamasika anasokonezekera, mukuwona, iwo amaikana manja pa wina ndi mzake ndi kuwapanga iwo aneneri ndi zina zotero. Tsopano, zimenezo si Mwamalemba. "Mphatso ndi maitanidwe sizimasowa kulapa." Iwe umabadwa uli chirichonse chimene iwe uli. Iwe unali, pachiyambi, chimene iwe uli.

Tayang'anani pa Afarisi aja mu masiku amene anapitawo. Iwo anali nako kuwala pang'ono chabe, chifukwa iwo amakhoza...anali ndi lamulo, ndipo iwo ankakhala moyo ndi lamulo, koma mu mtima mwawo umo munali mwakuda mmene mukanatha kukhalira.

21 Ndipo uko kunali mkazi wamng'ono, hule, zake... moyo wake wakale apa unali wakuda monga iwo ukanatha kukhalira, iye anali wambiri yoipa, koma pansu mu mtima mwake iye anakonzedweratu ku Moyo.

Ndiyeno pamene Yesu, Mawu, anabwera powonekera, Afarisi amenewo anati, "Munthu uyu ndi Bezebule." Kodi izo zinachita chiani? Izo zinadetsa kuwala kwapang'ono kumene iwo anali nako.

Yesu anati, "Ndinu wa atate anu, mdierekezi, ndipo zintchito zake inu mukuzichita."

Koma pamene mkazi wamng'ono uyu, woipa anabwera, ndipo iye anawawona Mawu a Mulungu, iye anawazindikira Iwo. Iye sankawakhala moyo Iwo, koma iye anawazindikira Iwo. Ndipo mwamsanga pamene Iwo anayankhula kwa iye, iye anati, "Ine ndazindikira kuti Ndinu Mneneri." Ndipo Iye... Iye anati, "Ine ndikudziwa kuti Mesiya adzachita izi."

Ndipo Iye anati, "Ine ndine Iye."

Kodi izo zinachita chiani? Izo zinayeretsa mdimawo ndi kuwupanga iwo onse kukhala woyera. Bwanji? Apo panali mbewu itagona pamenepo, mbewu yokonzedweratu imene inali mu...Ilo linali lingaliro la Mulungu asanaikidwe maziko a dziko lapansi.

22 Ulipo mtundu umodzi wokha wa Moyo Wamuyaya. Ngati inu muli nawo Moyo Wamuyaya, ndiye kuti inu eniake munali mu kuganiza kwa Mulungu dziko lisanalengedwe nkomwe. Ndinu gawo la kuganiza Kwake, chifukwa Umuyaya sunachite kuyamba kapena sungathe nkomwe. Inu nthawizonse, mwakhala muli gawo la chuma cha Mulungu. Izo zikungonyezimiritsa. Izo zikubwera tsopano. Iwo atsala ndi chithunzi chimodzi china kuti achitsuke, chimenecho ndi imfa, ndiye chithunzicho chikatsukidwa, ndiye kuti inu mudzapezeka mwa Mkwatibwi ndipo limodzi ndi Khristu, monga Iye anaganizira. Monga mwamuna ndi mkazi wake, lero, kotero (Mulungu) Khristu ndi Mpingo adzakhala zofanana. Tsopano, osankhidwa, oitanidwa!

Mose anabadwa, "mwana wabwinobwino." Baibulo limanena zimenezo.

Mmodzi wa aneneri, Yeremia. Mulungu anati, "Iwe usanawumbidwe nkomwe mmimba mwa amayi ako, ine ndinakudzozeratu iwe kuti udzakhale mneneri kwa fuko."

Yohane M'batizi, bwanji, iye anazindikiritsidwa mu Lemba. Yesaya, zaka seveni handiredi ndi thwelofu iye asanabwere, anati, "Iye ndi liwu la wina wofuula mu chipululu, 'Kudzakonzekeretsa njira ya Ambuye!'" Ndipo pafupifupi zaka foro handiredi Iye asanawonekere, kachiwiri ife tikupeza, Malaki akuti, "Taonani Ine ndidzatumia mtumiki Wanganga patsogolo Panga, kuti adzakonzekeretsa njira pamaso pa Ambuye."

23 Mukuona, iye anadzozedweratu. Ndipo chimodzimodzinso ndi maudindo onse awo a Mulungu, ngati iwo ali oitanidwa ndi Mulungu.

Ngati iwo aphunzitsidwira mwa izo, iwo amangokhala zakudya za akasinja, mukuona, izo sizingakhale chirichonse. Ngati icho chiri chitupa chodyera, ndiye kuti inu mwagulitsa ufulu wanu wakubadwa chifukwa cha chitupa chodyera, inu muzinyengerera kuti muziyenda ndi bungwe kapena gulu linalake. Koma ngati izo ziri za Mulungu, inu muima ndi Mawu amenewo, mulimonse, chifukwa inu munabadwa kuti mudzaima nawo iwo.

Mose, panalibe wina aliyense amene akanadzatzenga malo ake. Panalibe aliyense akanadzaichita ntchitoyo. Iye anadzozedweratu kuti adzaichite iyo.

Ndipo, abale, mlongo, ngati inu muli nawo Moyo Wamuyaya, inu munadzozedweratu kuti mudzachite chinthu chinachake. Mwinamwake mkazi wapakhomo wabwino, mwinamwake chinachakenso, koma palibe munthu amene angatenge malo anu. Mulungu anakonzekeretsa inu malo. Musamayesere kuti muzitenga malo a winawake. Kumeneko kukhala kutsanzira kwa chithupithupi, mukuona, zingasonyeze kuti pali chinachake cholakwika ndi inu. Muzikhala chimene inu muli, ndendende basi. Musakhale china chirichonsecho.

24 Tsopano, tsopano ife tikupeza kuti Mulungu anamupatsa Mose zizindikiro kuti akatsimikizire zozinenera zake ndi maitanidwe.

Ndipo chizindikiro choona chirichonse, chizindikiro choona chirichonse, chimene chatumizidwa kuchokera kwa Mulungu, chi...chimakhala ndi liwu kumbuyo kwa icho. Tsopano musalephere. Ili ndi phunziro langa lomaliza pa izi, mukuona. Chizindikiro choona chirichonse...Tsopano ife timakhala nazo zizindikiro zimene sizimakhala kuti ndi zochokera kwa Mulungu; Satana akhoza kutsanzira pafupifupi chirichonse chimene chiripo kumeneko. Koma chizindikiro choona, chotumizidwa kuchokera kwa Mulungu, chimakhala ndi liwu la Mulungu kumbuyo kwa icho.

Mulungu ananena ndi Mose, "Ngati iwo sakakhulupirira liwu la chizindikiro choyamba, ndiye ukachite chizindikiro china ichi pamaso pa iwo. Ndiyeno ngati iwo sakachimva ichi, ukangotenga madzi ndi kukawatsanulira iwo pa nthaka." Ndipo icho chinali chizindikiro kuti iwo akanadzanyowetsedwa uko mmagazi awo omwe.

Zindikirani, ndipo chimodzimodzi basi monga Iye ananena, "Mukasase fumbi pa mapazi anu. Zidzakhala bwinoko kwa Sodomu ndi Gomora, pa tsiku limenelo, kuposa mzinda uwo umene ukakukaneni inu."

25 Tsopano ife sitikuchita masanje a Tchalichi apa. Uwu ndi Mpingo. Khristu ndi Mpingo. Ife tiri mwa Khristu. Thupi lachinsinsi la Khristu, ife timabadwira mwa Iwo. Iwe sungathe kujowina Iwo.

Ine ndakhala ndiri ndi banja la a Branham kwa pafupifupi zaka fifite-faifi, ndipo iwo sanachite kundipempha ine kuti ndichite kujowina. Ine ndinabadwa ndiri Branham.

Ndipo umo ndi momwe iwe umakhalira Mkhristu. Iwe umabadwa uli Mkhristu, sumachita kujowinamo. Iwe umachita kubadwira mmenemo. Aliyense amachita mantha ndi kubadwa. Iwo ali nayo njira yina yabwino yogwirira dzanja laling'ono, kapena kulemba pa khadi laling'ono, kapena kukhutchumula mchere uli ndi madzi mmenemo. Kumeneko si kubadwa. Kubadwa ndi chinthu choipa kwambiri. Kubadwa ndi—chinthu cha nyansi. Ine sindikusamala ngati iko kuchitikira mu khola la nkumba, kapena—kapena modyera ng'ombe, kapena mu chipinda cha kuchipatala chokongoletsedwa mwa pinki; kubadwa ndi nyansi, ndipo izo zimakupangitsa iwe kukhala wa nyansi. Iwe sumafuna kuti usiye, iwe sumafuna ichi, icho, kapena chinacho, koma misonzi imatsuka zozipentapenta pa nkhope yako ndi kukupanga iwe munthu wosiyana. Ngati iwe wabadwanso kwatsopano, iko kumakupanga iwe kukhala wa wawutchisi, koma iwe umatulukapo uli cholengedwa chatsopano. Mukuona? Iwo samazifuna zimenezo. Iwo amafuna njira ina yophweka, inu mukudziwa, ndipo palibepo njira zophweka. Monga nyimbo ija, iye anati, "Ine ndidzatenga njira ya onyozeka ochepa a Ambuye." Iye samafuna kuti akhale kambewu kochita kupembedzedwa.

Chizindikiro choona chirichonse cha Mulungu chimatsatiridwa ndi liwu la Mulungu.

26 Tsopano ngati munthu apereka chizindikiro mu dziko, kapena pa nthawi iliyonse, ndipo liwu ilo limene iye akulankhula kumbuyo kwake siliri Mawu a Mulungu, ndiye muchiyang'anitsitse icho, musachikhulupirire icho. Ngati sukulu ina yakale, ngati munthu adzuka ndi kumanena, kumasonyeza chizindikiro chochokera kwa Mulungu, ndiyeno zimene munthuyo akuphunzitsa ndi zakusukulu ya zaumulungu yakale yomwe ija yomwe inu mwakhala nayo zaka zonse izi, Mulungu sanatume chizindikiro chimenecho. Mukayang'ansenso mu Lemba ndipo mukawone ngati izo zinakhalapo. Mukafufuze Lemba. Munthuyo akabwereranso, ndipo nkuti, "Tsopano ife tonse tiyenera kuti tijowine ichi. Icho ndi chinthu chokhazikitsidwa chakale." Inu musakhulupirire zimenezo. Ife tipita mu zimenezo, basi mu maminiti pang'ono, mwaona. Ayi, inu musakhulupirire zimenezo.

Mulungu nthawizonse amazitsimikizira zizindikiro Zake. Chizindikiro chochokera kwa Mulungu nthawizonse chimalankhula liwu la Mulungu.

Ndipo ngati ili sukulu yakale yomwe ija imene inu mwakhala muli nayo, ndi cha ntchito yanji kuti Iye akupatseni inu chizindikiro, inu muli kale mu zimenezo? Iye akuyesera kuti akutengereni inu pa ngodya imeneyo. Chizindikiro choimira! Chizindikiro chochepetsa liwiro! Muyang'ane kumene inu mukupita! Inu mukaziwunjika nokha pa ngodya ngati inu simukhala tcheru. Pali ngodya yokhota mosongoka, ndipo nthawizonse apo pamakhala chizindikiro inu musanakhote pamenepo, kukutetezani inu kuti musachite ngozi. Omanga msewu abwino amaika zikwangwani. Ndipo ife tikuyenda msewu wopita ku Ulemerero. Ndipo ngati chizindikirocho chikulankhula za chinthu chakale chomwe chija, icho sichinachokere kwa Mulungu.

Mulungu amapereka zizindikiro kuti zikope tcheru cha anthu Ake. Zizindikiro zimakhalapo kuti zikope tcheru cha anthu a Mulungu, ndiyo ntchito ya zizindikiro za Mulungu. Zizindikiro za Mulungu zimaperekedwa kuti zikakope tcheru cha anthu a Mulungu.

27 Tsopano apa chitsamba chonyeka chinali chizindikiro kuti chikakope tcheru cha mneneri, kuyesetsa, chifukwa mneneriyo anali atathawa kuchoka kwa Mulungu, ndipo Mulungu anapereka chitsamba chonyeka kuti chikakhale chizindikiro. Ndipo iye anawona chizindikiro chachilendo ichi; iye anati, "Ine ndipitoloka kuti ndikawone chimene chizindikiro chachilendo ichi chiri, kuti—chitsamba chikuyaka moto

ndipo icho sichikunyeka.” Tsopano Mulungu anali akukopa tcheru cha mneneri Wake wothawa. Iye akanakhoza kumutenga wina wake, koma iye anamudzozeratu Mose ku ntchitoyo ndipo panalibe wina aliyense amene akanadzatenga malo ake.

Ali mu ulendowo, anthu ena anayesera kuti achite zimenezo, inu mukudziwa. Datani anawuka ndipo ankafuna kuti apange bungwe pa izo. Mulungu anamuza Mose, “Udzipatule wekha. Ine ndingowameza iwo.” Mukuona?

Mulungu amachita ndi munthu payekha. Mukuona? Tsopano zindikirani ichi, Iye anali akuyesera kuti akope tcheru cha mneneri, kuti amutengere mneneriyo pa malo ake oyenera, mwaona, ndipo Iye anapereka chizindikiro cha chitsamba chonyeka.

Ndipo, penyani, liwu limene linkatsatira chizindikirocho linali liwu la Malemba. “Ine ndamva kulira kwa anthu Anga, ndi kubuula kwawo, chifukwa cha owagwiritsa ntchito, ndipo Ine ndakumbukira lonjezo Langa.” Ameni. Izo zikukhazikitsa izi. “Ine ndakumbukira lonjezo.” Limenelo linali liwu la Mwamalemba. “Ndipo Ine ndikukutuma iwe kumeneko. Ine ndatsika kuti ndidzawawombole iwo, ndipo Ine ndikukutuma iwe.”

28 Kumbukirani, Mulungu samachita kanthu kunja kwa munthu. Inu mukudziwa zimenezo? Izo ndi zimene zimawaphunthwitsa anthu. Mukuona?

Ndi zimene zinawaphunthwitsa iwo za Yesu. Iwo ankati, “Ndiwe Munthu, ukudzipanga wekha kukhala Mulungu.” Iye anali Mulungu, koma iwo samatha kuzimvetsa zimenezo. “Chabwino, Iwe, wangokhala Munthu.”

Iye anati, “Chabwino, inu mumawatcha aneneri, 'milungu,' ndipo lamulo lanu limazizindikira izo. Ndipo ngati inu mumawatcha iwo 'milungu,' amene Mawu a Mulungu anadzako, inu mungandiweruze Ine bwanji pamene Ine ndikuti ndine Mwana wa Mulungu?”

Mukuona, zizindikiro, kuti zikakope tcheru. Ndipo, kumbukirani, ngati tcherucho chakopedwa, ukakhala mzere wakale womwe uja, ameneyo si Mulungu.

Koma Mulungu akuyesera kuti amukope mneneri tsopano, ndipo Iye akumupatsa iye chizindikiro, ndipo liwu limene linkatsatira chizindikirocho linali liwu la Mwamalemba. “Ine ndawawona anthuwo. Ine ndamva za kulira kwawo. Ine ndikukumbukira lonjezo Langa.”

29 Tsopano Mulungu alankhula mwa Mawu Ake olonjezedwa. Iye ayenera kuti amutumize mneneri Wake, chifukwa Mawu amadza kwa mneneri. Baibulo limatero, Mulungu anatero, Mwiniwake, kuti, “Iye samachita kanthu kupatula Iye ataululira izo kwa antchito Ake aneneri poyamba.” Mukuona? Ndipo kenako chizindikiro chimaperekedwa. Ndipo Lemba limazindikiritsidwa, limenelo ndiye Liwu la chizindikiro.

Mwaliwona Liwu la chizindikiro, la Mose? Poyamba, chizindikiro chinali chitsamba chonyeka; Liwu linali Lemba.

Mose anachitenga chimenecho ngati chizindikiro Chake, ndipo anapita uko ku Igupto ndipo anakachita chizindikiro chimene Mulungu anamuza iye; ndipo chizindikirocho chinali ndi liwu kwa icho, ndipo anthuwo anakhulupirira ndipo apa anali akutuluka. Ndipo nthawizonse pamene amayenda, iwo anali akuchita bwino; koma pamene iwo anayamba kung'ung'uza motsutsana ndi liwulo, ndiye iwo ankaima.

30 Kumbukirani, Israeli amayenda. Kodi inu mukudziwa kuti iwo anafika mpaka pati? Iwo bwezi ali...Iwo anali kokha mailosi forte, ndipo pafupi zaka forte akuchita zimenezo. Bwanji? Ndi chifukwa chakuti iwo anayamba kung'ung'uza motsutsa liwu limene linkapereka chizindikirocho. Iwo ankadziwa mwapang'ono bwanji, pamene iwo anali akufuula kumusi uko pa magombe, ndi kumavina mu Mzimu, ndipo Mose akuimba mu Mzimu, iwo anali kokha masiku pang'ono kuti akafikeko. Koma iwo anayamba kung'ung'uza, ndipo ankafuna kuti achite chinachake chosiyana; ndipo iwo anakhala zaka forte ali mu chipululu, ndipo anafera momwemo, ndi zoonza zimenezo, chifukwa iwo sankakhulupirira. Mulungu anati, “Iwo sakutsutsana ndi iwe, Mose. Iwo akutsutsana ndi Ine.” Limenelo linali liwu la Mulungu, osati Mose.

31 Tsopano penyani, Yehova alankhula mwa Mawu Ake olonjezedwa, kotero Iye ayenera kuti atumize aneneri Ake. Zimenezo, ngati inu mukufuna kuti muziwone zimenezo, zimenezo ziri mu Genesis 15:16. Ife tikupeza kuti Mulungu anamuza Abraham, “Mbewu yako idzakayenda mu dziko lachirendo, ndipo Ine ndidzakawatulutsako iwo ndi dzanja lamphamvu. Kusaweruzika kwa Amori sikunakwanirebe.” Malonjezo Ake onse amene Iye anawapereka, apa Iye akumukopa mneneri, ndi chitsamba chonyeka.

Tsopano ngati chitsamba chonyeka chikanati, “Mose, Mulungu ndi Mulungu.”

“Eya, ine ndikukhulupirira zimenezo.”

“O, iwe ukuchita bwino, Mose, kazipitirira nazo zimenezo. Iwe unakwatira mkazi wabwino; iyeyo ndi mwana wokongola. Zedi uli ndi mwana wamwamuna wabwino! Ulemerero kwa Mulungu!” Imeneyo ndi

sukulu yakale yomwe ija. Mukuona? Koma Iye anali atakonzeka kuti achite chinachake, kotero Iye ankayenera kuti amukope munthuyo. Ndipo Iye anamupatsa munthuyo zizindikiro ziwiri zoti achite, ndipo anati, "Chizindikiro chirichonse chinali ndi liwu." Izo zimatsimikizira kuti izo ziri chomwecho. Tsopano penyani zomwe maliwu amenewo ankalanikhula, ngakhale mpaka kulenga. Yehova anali atakonzeka kuti alankhule tsopano.

32 Kachiwiri, kubwera kwa mneneri ndi chizindikiro. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Kubwera kwa mneneri, ku m'badwo, ndi chizindikiro.

Tsopano, ine sindikutanthauza Dokotala wa Zaumulungu. Ine sindikutanthauza m'busa wina wokhulupirika, munthu wina wabwino. Zimenezo ndi zabwino. Amenewo ndi antchito a Mulungu.

Koma mneneri ndi chizindikiro. Baibulo likunena zimenezo apa. Ndipo kodi ndi chizindikiro cha chiani? Ndi chizindikiro chakuti Mawu Ake akukonzekera kuti akwaniritse, kuti akwaniritsidwe mwa liwu la chizindikiro cha mneneri uyu.

Zindikirani, kubwera kwa mneneri ndi chizindikiro cha kuchenjeza za chiweruzo chimene chiri pafupi. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Chiweruzo chikukonzekera kuti chikanthe ngati muli mneneri mu dzikolo.

Kumbukirani, iyeyo motsimikizika, poyamba, ayenera kuti avomerezedwe ndi Mulungu ndi Mawu a tsiku limenelo, ndipo kenako iye achita chizindikirocho. Ndiyeno mupenyetsetse chizindikiro chimenecho, zimene iye akuneneratu. Iye anati, "Ngati izo zifika podzachitika, ndiye mumumvere iye." Numeri 12:6. "Ngati izo sizidzafika pochitika, ziiwaleni zimenezo." Icho chiyenera kukhala chizindikiro cha Mwamalemba chimene Iyeyo akupereka.

Ndipo chimene Iye anaperekera ngati chizindikiro, nthawi ina, ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, Iye mosalekeza amakhala akupereka icho chimodzimidzi. "Mawu a Ambuye amadza kwa aneneri." Iwowo amakhala ali Mawu. Ndipo pamene Yesu anabwera, Iye anali Mawu. Ndipo Mawu ankazindikira malingaliro ndi zolinga za mtima, mosalekeza, pang'ono ndi pang'ono. Tsopano penyani.

Kubwera kwa mneneri uyu, kumapereka chizindikiro, chakuti, "chiweruzo chiri pafupi," nthawizonse.

33 Tiyeni tingoima kwa pafupi maminiti pang'ono. Ine sinditenga nthawi yotalika kwambiri. Tiyeni tingofufuza zingapo tsopano, kwa pafupi maminiti khumi. Ndipo uthenga wonsewo, kani, kwa maminiti khumi.

Nowa, mneneri pa dziko—mu dziko, chizindikiro cha chiweruzo chimene chikubwera. Mose, mneneri mu dziko, chizindikiro cha chiweruzo chimene chikubwera. Eliya, mneneri mu dziko, chizindikiro cha chiweruzo chimene chikubwera. Yohane, mneneri mu dziko, chizindikiro cha chiweruzo chimene chikubwera kwa Israeli; iwo mwamtheradi anali atadulidwa.

Zindikirani, chizindikiro! Kodi chizindikiro chimachita chiani? Chizindikiro chimakopa tcheru, ndipo chimawakonzeketsera osankhidwa, ndi kuwachotsapo panjira chiweruzo chisanakanthe. Ndi chimene Nowa anachita, anawakonzeketsera osankhidwa. Ena onse a iwo, ndipo kodi icho chimachita chiani? Chizindikiro, ndi liwu la chizindikiro, zimamuweruza wosakhulupirira ndi kumukonzeketsera iye ku chiweruzo. Izo zimawakonzeketsera osankhidwa kuti athawe. Ndiyo ntchito ya chizindikiro. Ndi chifukwa chimene zizindikiro zimaperekedwera, chifukwa cha chiweruzo chimene chikudza. Kwa osankhidwa, iwo amachiwona icho.

34 Monga mkazi wamng'ono wa mtima wangwiro, ndi thupi lodetsedwa; ndi Mfarisi wa thupi langwiro, ndi mtima wodetsedwa. Icho chinamuweruza wina, ndi kumupulumutsa winayo.

Ndipo ziweruzo zomwezo zimene zinamupulumutsa Mose, zinaliweruza dziko; kulalikira kwake.

Icho chimamukonzeketsera wosankhidwa. Kodi wosankhidwayo azikonzekera chiani? Pamene iwo achiwona chizindikiro chotumizidwa ndi Mulungu, iwo amayang'ananso mmbuyo mu Lemba ndipo amawona ngati zimenezo zimayenera kuti zikakhale pamenepo. "Eya, ndi izi apa." Ndichiani izo? Chiweruzo chimene chikubwera. Ndiye osankhidwawo amamvera kwa liwulo.

Koma osasankhidwa amanyalanyaza, ndikuti, "Zamkutu. Kazipitirirani! Ife titenga sukulu yakale yomwe ija." Mukuona? Umo ndi mmene iwo anachitira mmasiku a Lutera. Umo ndi mmene iwo anachitira mu masiku a Wesile. Umo ndi mmene iwo—iwo akuchitira tsopano, mmene iwo akhala akuchitira nthawizonse.

Koma icho ndi chizindikiro, ndipo icho chiri nalo liwu limene likutsatira chizindikirocho. Ndipo liwulo limazindikiritsidwa ngati liwu la Mwamalemba. Tsopano musaiwale zimenezo. Tsopano mulole zimenezo zizilowelera, chifukwa mwina ine sindidzakuwonaninso inu.

Ine ndikukhumba ndikanakhala nayo njira imene ine ndingadzathe kubwereranso kuno kwinakwake ndi kudzawatengera abale anga onse, pamene iwo alibe zitsitsimutso zimene zikuchitika, ndikudzazika hema

ndipo ndikudzangokhalapo, tsiku ndi tsiku, ndi kudzaphunzitsa izo mpaka—mpaka izo zitalowerera kwenikweni. Koma Iye sangaloleze zimenezo, ine sindikuganiza. Mukuona, ife tiri pafupi zedi ndi kumapeto. Ine ndikukhulupirira kuti ife tiri pakali pano kumapeto.

35 Mu bukhu langa umo, limene ine ndikumalilembabe. Mu 1933, mmawa wina, ndikukonzekera kuti ndizipita ku Sande sukulu, Sande sukulu ya Chibaptisti kumene ine ndinali m'busa, Mzimu Woyera unabwera ndipo unadzandisonyeza ine mpaka ku nthawi yotsiriza, ndipo unadzandisonyeza ine zinthu zisanu ndi ziwiri zimene zikanadzachitika. Ine ndinazilemba izo. Ziri pa pepala lachikasu lakale.

Anandiuza ine ndendende momwe Germany akanadzamangira Mzere wa Siegfried, ndi momwe Achimereka akanadzamenyedwera pa iwo, zaka leveni iwo—mzerewo usanamangidwe nkomwe.

Ananena momwe Mussolini akanadzadzukira, ndi momwe iye akanadzapitira ku Ethiopia, ndi momwe Ethiopia “akanadzagwera pa mapazi ake.” Ndi momwe iye akanadzafera mwamanyazi, adzatembenuzidwire chadodolido, ndipo anthu ake omwe akanadzamulavulira iye.

Ndipo ine ndinati, “Pali ma ism atatu; Kominisi, Facism, ndi Nazism. Zonsezo zidzathera kwa Russia, mu Chikominisi.” Ndipo icho chidzawononga Chikatolika. Muwone ngati izo sizikutero!

Ine ndinati, “Padzakhala kutukuka komwe kudzachitike!” Ine ndinati, “Ine ndikuwona magalimoto owoneka ngati dzira, akuyenda mu msewu. Pali magalimoto akuyenda mmisewu yaikulu, yokhala ndi kena koyendetsera, iwo sakusowa kumachita kuiwongolera iyo. Ine ndinawona banja la Chimereka likusewera tchesi kumbuyo kwa galimotoyo.” Iwo ali nayo galimotoyo pakali pano, ngati iwo akanangokhala nayo misewuyaikulu kuti akaiyikemo iyo. Volkswagen yaing'onoyi ndi dzira basi, ndendende basi, ndi magalimoto ena onsewa. Kodi inu mungalingalire, mu 1933, kuti magalimoto ankawoneka ngati chiani, mutafanizitsa ndi pano?

36 Ndiyeno Iwo unaneneratunso, za, kuwaloleza akazi kuti azivota, ndi zomwe iwo adzachte. Ndi momwe dziko lino, pokhala choimira, monga Israeli, anabwera mu dziko ndipo anadzawathamangitsa okhalamowo, ndipo anadzalitenga dzikolo. Ndipo mafumu apang'ono oyamba amene iwo anali nawo, Davide ndi Solomoni, anali mafumu owopa Mulungu. Patapita kanthawi, iwo anamutengera Ahabu powonekera. Iwo anamuvoteramo iye. Mpandowo udzafika...mpingowo unadzakhala mwachidziko. Ndipo, ife tinali naye Lincoln ndi Washington, muwone zimene ziripo lero. Muwone kumene ife tikupita tsopano. Kodi chinthu chotsatira chiri kuti? Ife tiri pamapeto a nthawi.

Ndipo icho ndi chizindikiro, mu chithupi, ndendende basi. Izo zikumukonzeketsera wosankhidwa; ndi kumuweruza, waku chiweruzo, wosakhulupirira.

“Ngati mneneri uyu ali mneneri woota, ndipo zimene akunenera zikumachitika,” Baibulo linati, mu Numeri 12:6, “mumvere chenjezo lake, chifukwa izo zatsimikiziridwa kuti si munthuyo ayi.” M—mneneri ndi munthuyo. Koma liwu limene likuchokera ku chizindikiro chauzimu ndi liwu la Mwamalemba, ndi lotsimikiziridwa, ndiye ndi chenjezo.

Baibulo linalembedwa ndi aneneri, muzikumbukira. Mu Petro Wachiwiri, aponso, 1:21. Mu Ahebri 1:1, aponso.

37 Lawi la Moto, kwa Mose, linali chizindikiro, liwu linali loti liyankhula. Lawi la Moto linkasonyeza kuti liwu liyankhula. Chimenecho ndicho chizindikiro, Lawi la Moto. Anthu inu muyenera kuti muzikumbukira zimenezo kuchokera ku Houston, osati kale litali.

Mose, mneneri, chizindikiro kwa Israeli, kuti lonjezo linali litangotsala pang'ono kuti likwaniritsidwe. Pamene Mose anabwera ndi kudzachita chizindikiro cha mneneri, iwo anadziwa nthawi yomweyo kuti iye awasonkhanitsa iwo palimodzi.

Mawu a Mulungu amakhala angwirowanji mwa dongosolo, nthawi iliyonse chimodzimidzi. Ngakhale monga ine ndinanena usiku wathawu, momwe Urimu Tumimu, ndi chirichonse, nthawizonse zakhala zikuyankhira kwa Mulungu.

38 Tiyeni timutengenso mneneri, mphindi chabe, Yona. Ine ndinali ndi mutu woyamba wa Yona ndinalimba apa, mutu Woyamba apa wa uneneri wake. Yona anabwera kuchokera mmimba ya nsomba, anali chizindikiro. Mukuona, anthuwo anali achikunja. Iwo ankapembedza milungu ya mnyanja, ndipo mulungu wawo wa mnyanja inali nsomba yaikulu.

Tsopano anthu ambiri amayesera kuti azimuweruza Yona. Ine nthawizonse ndimamuikira kumbuyo Yona. Yona sanachoke mu chifuniro cha Ambuye. “Mapazi a olungama amatsogozedwa ndi Ambuye.” Ife tikufuna kunena kuti, “Uyu ndi Yona.” Koma tiyeni tingozitenga izo momwe... momwe uliri mtengo wake, mwa kamodzi. Ine ndikudziwa kuti iye anayenera kuti apite ku Nineva, koma Mulungu anamutengera iye ku ngalawa ija ya ku Tariso. Ndipo Iye anabweretsa vuto pa nyanjapo.

Yona anati, “Mundimange manja ndi miyendo. Ineyo ndi amene ndiri mu vuto, ndi amene ndapangitsa

zimenezi.” Ndipo anamuponyera iye panja. Ndipo nsomba inali ikusambira mmadzimo, nsomba yaikulu, imene inamumeza Yona. Ine ndikudziwa kuti zimenezo ndi zovuta kuti sayansi ikhulupirire.

39 Kuno osati kale litali, mu Louisville, Kentucky, pafupifupi zaka khumi zapitazo, iwo anali ndi—nsomba itagona pa—pa galimoto. Ndipo pamenepo panali ka Ricky kena kakang'ono pamenepo, kanali ndi luntha lochuluka lomwe kamalephera kuti kalilamulire. Iye anali akuyesera kuti alipangitse Baibulo kuti limanena zabodza. Iye anati, “Inu mukudziwa, inu mumamva mwambi wakale wa Baibulo uja, kuti nsomba inamumeza Yona.” Iye anati, “Taonani, iwe sungaike mpira kuwudutsitsa pa mmero wake, iyo inali yaing'ono kwambiri. Zingatheke bwanji kuti munthu wachikulire apite mmimba mwake?” Anati, “Inu mukuona, iwo ndi mwambi wachikale basi, monga Baibulo lazadza ndi zoterozo.”

Zimenezo zinali zondichulukira kwambiri mwa—mwa maganizidwe anga. Ine ndinati, “Bwana, ine ndikufuna kuti ndinene chinachake pamenepo.”

Anati, “Inu mukufuna kunena chiani?”

Ine ndinati, “Inu mukuona, inu simunawerenge bwino Baibulo.” Ine ndinati, “Baibulo limanena kuti iyi inali nsomba yapadera. 'Mulungu anaikonza nsomba yaikulu.' Iyi inali yowumbidwa mwapadera, kuti ikamumeze iyeyo, izo zinamuleketsa iye! Iyo siinali nsomba wamba. Mulungu anali woti akukachita ntchito yachilendo, kotero Iye anapeza nsomba yachilendo.” Mukuona? Iye sananenenso kalikonse za izo pamenepo. Kotero, iyo, Mulungu anali nacho chinthu chapadera.

40 Monga msungwana wamng'ono, nthawi ina, akubwera kuchokera ku kachisi; tsitsi lake lapang'ono atalipesera mmbuyo, ndiponso lonyololoka, mokwanira mpaka nkhope yake yaing'ono inkawoneka ngati anyezi wosendedwa. Iye anali atanyamula Baibulo, akupita kumusi.

Bambo wachikulire uyu dzina lake Jim Dorsey ankakhala ku Utica. Iye anali wachikunja, msilikari wakale, ndipo—ndipo iye sankakhulupirira Mulungu. Ndipo iye anati, “Kodi iwe ukupita kuti, dona wamng'ono?”

Iye anati, “Ine ndikupita kwathu, bwana.” Anati, “Ndi chiani wanyamula mdzanja lako?” Iye anati, “Ndi Baibulo.”

Anati, “Iwe sumalikhulupirira ilo, ndi choncho iwe?” Ndipo iye...

Anati, “Inde, ine ndimalikhulupirira ilo, bwana.”

Ndipo anati, “Kodi iwe umakhulupirira nkhani ija mmenemo ya nsomba kumumeza Yona?”

Anati, “Bwanji, zedi, ine ndimakhulupirira Mawu aliwonse a ilo.”

Iye anati, “Kodi iwe ungazitsimikizire izo motani mwanjira ina iliyonse kupatula chikhulupiriro, chimene inu mumachitcha chikhulupiriro?”

“Bwanji,” iye anati, “ine ndikadzafika Kumwamba, ine ndidzakamufunsa Yona.” Mukuona?

Iye anati, “Ndiye nanga bwanji ngati iye sakakhalako kumeneko?”

Iye anati, “Ndiye inu muyenera kuti mudzakamufunse iye.” Chotero ine ndinaganiza icho chinali chowongolera chabwino kwambiri. Chotero ine ndikuganiza kumeneko ndiye kulondola kwake.

Ngati Baibulo likananena kuti Yona anameza chinsomba, ine ndikanazikhulupirira zimenezo. Iye akanazikonza zimenezo. Zimene Mulungu wanena, Mulungu ndi wokhoza kuti azichite, ndipo Iye nthawizonse amasunga Mawu Ake. Kotero, Yona, ife timamuseka iye...

41 Koma kodi inu munayamba mwaiwonapo nsomba pamene iyo ikusambira? Iyo ikamasaka chakudya chake. Ndiyeno pamene iyo yadya, iyo imapita pansu pomwe ndipo imakapumitsa zosambilira zake zazing'ono pansipo. Mudzaidyetse nsomba yanu ya mbuna ndipo mudzawone zimene zinachitika. Izo zimazadzitsa mimba zawo mokhuta, ndiye izo zimapita pansu ndipo zimakaika zosambirira zake nkuzisamiritsa pansipo, ndipo zimakagona pamenepo ndi kumapumulira kaye.

Chabwino, nsomba yochita kukonzedwa yaikulu iyi inabwera pamenepo ndipo inadzamumeza mneneri uyu. Ndipo iyo inapita pansu pomwe pa nyanja, ndipo mwinamwake utali makumi anai kuya kwake pamenepo. Iyo inapita pansu patali, kuti ikazipumitse yokha pansu pa nyanja.

42 Tsopano ife nthawizonse timakhala tikuganiza za Yona. Ndipo aliyense amati, “Tsopano ine ndinapemphereredwa, koma dzanja langa siliri bwino. Ine ndinapemphereredwa, koma ine sindikumvabe bwino.” Inu musamakuwe nkomwe za Yona.

Tsopano taonani zomuchitikira zowoneka zimene iye anali nazo. Tsopano, kuyamba ndi kuyamba, iye anali pa nyanja ya namondwe, ndipo iye anali atachoka pa ntchito imene Mulungu anamutumirako iye.

Manja ake ndi miyendo zinali zitamangidwa. Iye anaponyedwera mu nyanja itachita ukali, ndi namondwe, ndipo chinsomba chinamumeza iye ndipo anapita pansi pomwe pa nyanja. Ndipo iye anali atagona pamenepo mu masanzi, mmimba mwa chinsomba, anamasupuni atazengeza khosi lake. Ndipo iye akayang'ana mbali iyi, munali mmimba mwa chinsomba. Iye akayang'ana mbali iyo, munali mmimba mwa chinsomba. Kulikonse kumene iye amayang'anako, munali mmimba mwa chinsomba. Inu mukanena zochitika zowonekera, iye mwina anali nazo izo. Koma inu mukudziwa zimene iye ananena? Iye anati, "Izo ndi zopanda pake. Ine sindiyang'ananso pa izo, koma kamodzinsu ine ndiyang'ana ku kachisi Wanu woyera."

Chifukwa, Solomoni, munthu wachibadwa wa dziko lapansi, amene anapemphera pomupereka kachisi, anati, "Ambuye, ngati anthu Anu akadzakhala mu vuto kulikonseko, ndipo akadzayang'ana ku malo oyerawa, ndiye mudzawamve kuchokera Kumwamba."

43 Ndipo Yona anali nacho chikhulupiro mu zimene Solomoni anali atapemphera. Ndipo Mulungu anamupulumutsa iye kuchokera mu chinsombacho, atatha masiku atatu ndi usiku. Iye mwina anayika hema ya mpweya pansi pamenepo. Ine sindikudziwa zimene Iye anachita, koma Iye anamusunga ali wa moyo kwa masiku atatu ndi usiku, molingana ndi Mawu. Ndipo Mawu ndi owona.

Chabwino, ngati Yona, pansi pa zomuchitikira zimenezo, anatha kuyang'ananso ku kachisi amene munthu anamupanga, ndi mochuluka bwanji tiyenera inu ndi ine, usikuuno, kuti tiziyang'ana ku Kachisi kumene Yesu akuima pa dzanja lamanja la Ufumu, ali ndi Magazi Ake Omwe, akupembedzera pa zodzinenera zathu, pa zotichitikira zathu zapang'ono! Musamamuweruze Yona, kenako nkuyang'ana pa zimene zalakwika ndi inu. Muziyang'ana kwa lonjezo, "Mulungu ananena zimenezo!" Ngati ndinu ana a Abrahamu, "Mulungu ananena zimenezo!" Iye anapanga lonjezo, ndipo izo zikukhazikitsa zimenezo.

44 Zindikirani, anthu onse anali ali uko akuwedza, ndipo akukoka nkhoka zawo ndi zinthu. Patapita kanthawi, panatulukira mulungu-wa mnyanja, chinsomba, chikuthamangira ku gombe. Aliyense anagwa pa mawondo awo. Mulungu amadziwa kuchita zinthu. Ndipo icho chinafika mpaka ku gombe ndipo chinatulutsa lirime lake, ndipo, pamene icho chinatero, apa panabwera mneneri akuyenda akutuluka kumene kuchokera nkamwa mwa chinsombacho. Mneneri! Mulungu anakumulavula mneneri pa gombelo. Nzosadabwitsa kuti iwo analapa. Mukuona?

Chimenecho chinali chizindikiro. Yona powomboledwa ndi chinsomba, chinali chizindikiro. Kodi iye anachita chiani? Chimenecho chinali chizindikiro chochokera kwa Mulungu. Kodi liwulo linati chiani? "Lapani kapena muwonongeka, mu masiku makumi anai." Chizindikiro cha Mulungu; liwu la Mulungu! Nthawizonse, pamene Mulungu atumiza chizindikiro, Mulungu amatumiza liwu Lake kumbuyo kwa chizindikiro chimenecho. Zindikirani, "Lapani, kapena mu masiku makumi anai mzinda wonsewu uwonongeka."

45 Yohane mneneri kuwonekera pa dziko lapansi, patatha zaka foro handiredi pasanakhalepo mneneri; chizindikiro patatha zaka foro handiredi, za kuwonekera kwa iye. Nthawi yapang'ono yolekerera ija!

Tsopano ngati ndinu auzimu inu mumvetsa zimene ine ndikunena. Mulungu atsegule kumvetsa kwanu. Kodi zakhala nthawi yotalika bwanji!

Zaka foro handiredi, Israeli anali alibe mneneri, mipingo inali itapotozedwa kwambiri, ndiyeno apa panabwera Yohane pa chochitikacho. Yohane anali mneneri, chizindikiro chakuti Mesiya akanadzayankhula akachokapo iyeyo. Penyani. Chifukwa, Malaki 3 anati, "Ine ndidzatumiza Mtumiki Wanga pamaso Panga, kuti adzakonzeketsere njira, adzawakonzeketsere anthuwo."

Tayang'anani pa Yohane, analibe kuzikonda mwa iye. Iye sanadzitengere ulemerero uliwonse. Iwo anayesera kuti amutche iye Mesiya; koma iye anati, "Ine sindine woyenera kumasula zingwe za nsapato Zake."

Koma mwamsanga pamene Yesu anawonekera, Iye anali ndi chizindikiro, Lawi la Moto, Kuwala pamwamba pa Iye, kofanana ndi nkunda kunabwera ndi liwu lakuti, "Uyu ndi Mwana Wanga wokondedwa, Amene Ine ndikukondweretsedwa naye."

Zindikirani, ndipo Yohane nthawi yomweyo anati, "Iye ayenera kuti akule. Ine ndiyenera kuti ndichepe." Iye anawupereka Mpingo kwa Khristu. Amen.

46 Ife tikuwuzidwa kuti, mu masiku otsiriza, zimenezo zidzabwereza kachiwiri! Padzakhala Uthenga umene udzabwere, umene uti udzamuwonetsere Mesiya kwa anthu. Ndipo izo zidzakhala mwanjira yakuti, iwo adzaima ali kakasi monga iwo anachitira nthawi ijayi. Iye analonjeza zimenezo. Mutu wotsatira wa Mateyu, wa Malaki, amatiuza ife za zimenezo. Penyani.

Iwo anafunsa za izo. Chikhalidwe cha Yohane chinamuzindikiritisa iye mu mzimu wa Eliya. Tsopano zindikirani aneneri awiriwo.

Tsopano, Eliya anali munthu amene anawuka mu nthawi ya Israeli, mu chisokonezeko.

Ahabu anali mfumu. Ndipo akazi onse anamutsanzira Yezebeli, ndipo mwinamwake amadula matsitsi awo mwaphanke ndi chirichonse, mwinamwake monga momwe ife tiri nazo lero. Ndipo onse anamutsatira Yezebeli. Ndipo azibusa ankaganiza, "Kuti zimenezo zinali zabwino basi. Asiyeni iwo okha. Asiyeni iwo azichita zimenezo."

Ndipo pa nthawi imeneyo, Mulungu anadzutsa mwamuna kuchokera ku chipululu, dzina lake Eliya. Iye sitimadziwa nkomwe kumene iye anachokera. Iye analibe sukulu yoti imuzindikiritse iye. Koma iye anauka, ndipo iye anadzudzula chinthu chonse icho. Iye anadzudzula kachitidwe konseko.

Ngati iye angabwere powonekera, lero, iye akhoza kudzudzula kachitidwe kathukanso. Iye anamudzudzula Yezebeli aliyense. Ndipo izo, potsiriza, anali iyeyo amene anamuwopsyeya mneneri. Anathawa, monga Yohane; anakagona pansu pa mtengo wa tsanya pamene Yezebeli ankapita kuti akamuphe iye. Iye ankamuda iyeyo.

47 Ndiyeno ife tikupeza kuti pamene Yohane anabwera, kuchokera ku chipululu kachiwiri, wokonda chipululu, ali ndi uthenga wolunjika kwa akazi amakono okhala atasudzulidwa chikwati ndipo nkukwatiwanso, ndi kukwatiwanso, iye anachidula chinthucho mzidutswa. Iye sanabwere kuchokera ku sukulu iliyonse. Iye anabwera kuchokera kwa Mulungu, munthu wotumizidwa kuchokera kwa Mulungu. Ndipo iye anawadzudzula akazi amakono, anawatsutsa iwo molimba, ndipo iye sanabweze nk'honya zirizonse. Koma mwapoyera ankati, "Nthawi ili pafupi, Mesiya ayankhula." Taonani zimenezo.

Tsopano mufanizitse nthawi ya kubwera koyamba kwa Eliya ndi ena a aneneri amakono awa a lero, ololeza Ayezebeli awo kumadula tsitsi lawo, ndi kumavala akabudula, kumasuta ndudu, chirichonse chimene iwo akufuna kuti achite, kumawatsogolera iwo paliponse. Kulibwino asanene kanthu, amusiya iye, akapeza wina. Kumawatsogolera iwo ndi tizikhulupiro topangidwa ndi anthu; zimenezo ndi zamanyazi, ziphunzitsa za munthu. Ndipo, pakuchita zimenezo, iwo akuwapangitsa malamulo a Mulungu kukhala opanda mphamvu, chifukwa iwo akhoza kujowina mpingo ndi kumadzinenerabe kuti iwo ndi Akhristu, ndi kumachita zofuna zawo ndi kumanena kuti iwowo ndi Akhristu, ndi kumapitirirabe. Ndizo zimene iwo akuzifuna. Ndizo zimene iwo ankachita kumeneko.

Koma, kumbukirani, ndi pa nthawi yonga imeneyo, monga Mulungu analonjezera mu Malaki 4, kuti Iye akanadzakwaniritsa Mawu kachiwiri. Ndiko kulondola. Taonani pamene ife tiri lero, basi monga izo zinaliri mu nthawi ya Yohane, basi monga izo zinaliri mu nthawi zinazo.

48 Tamuwonani Amosi wamng'ono wakale uyu akuwuka, kamunthu kakang'ono kokalamba. Iye sitikudziwa kumene iye anachokerako. Iye anali woweta ziweto. Mulungu anali akumuchotsako iye ku msipu wa nk'hosa ndi msipu wa ng'ombe, ndi, ndipo ankakamuphunzitsa iye. Ndipo pamene iye anafika ku Samaria, ndipo pamene iye anadzuka ndipo nakwera phiri limenelo tsiku lijali, anakayang'ana pansu apo. Ndipo dzuwa lija likuwalira pa mutu wake wa dazi, ndipo manyenje ake ali otuwa, ndi maso ake okhazikika ndi onyezimira. Maso ake aumulungu anaphethira, osati chifukwa cha mawonekedwe amene anthu odzawona malo ankawona pamene iwo amabwera mmenemo, chifukwa chakuti mzinda wonsewo unali utadzipereka kwa tchimo.

Ndi ndani munthu wamng'ono uyu, wosadziwika? Inde, ndi Amosi, mneneri. Iye analosera mu masiku a Yeroboamu Wachiwiri, mfumu ya uchigawenga, ankawaloleza anthu kuti azichita zirizonse. Ansembe onse anali mu zimenezo. Iwo anamanga mipingo yokongola kwambiri. Iwo anali ndi mavalidwe abwino. Akazi awo anali opanda makhalidwe. Iwo ankavala mulimonse momwe iwo afunira. Oyenda odzawona malo ankakhamukira paliponse, kuti adzawone asungwana okongola ndi zochita zawo.

Basi U.S.A. wina wamakono, ankayenera kuti akhale anthu a Mulungu. Palibe aliyense ankanena kanthu za zimenezo. Izo zinkawoneka kuti zinali zowalamulira pa anthuwo. Fifi...

Zaka eyitini tsopano, lero! Rebekah wanga ali usinkhu wa zaka eyitini, lero. Zaka eyitini, ine ndakhala ndikudutsa fuko lino, ndikudzudzula zinthu zimenezi. Ndipo ine ndikamabwerera, chaka ndi chaka, kukumakhala akazi odula tsitsi ambiri kuposa amene analipo nthawi yoyamba pamene ine ndinkayamba.

49 Mlaliki wotchuka, wodziwika wachi Pentekoste ananditengera ine mchipinda, pafupi chaka chathacho, wabwino, wodziwika-bwino, munthu wodziwika pa dziko lonse. Iye anati ine..."M'bale Branham, mundilole ine ndiyike manja anga pa inu ndipo ndikupempherereni inu."

Ine ndinati, "Ine sindikudwala."

Iye anati, "Koma pali chinachake cholakwika." Iye anati, "M'bale Branham, inu muwononga utumiki wanu. Palibe aliyense azigwirizana nanu. Nzosadabwitsa azilaliki sakumagwira nanu ntchito; ndi mmene inu mukuwadzudzulira akazi amenewo."

Iye anati, "Anthu amenewo amakutchani inu mneneri."

Ine ndinati, "Ine sindinayambe ndanenapo kuti ine ndinali."

Iye anati, "Koma iwo amaganiza kuti inu muli." Iye anati, "Ine ndimakhulupirira chinthu chomwecho." Iye anati, "Inu munaitanidwa kuti muzidzawapempherera odwala." Iye anati, "Kazipemphererani odwalawo, ndipo asiyeni akazi amenewo okha. Inu mukumawapweteka kumverera kwawo."

Ine ndinati, "Motani?"

Iye anati, "Mukamalankhula zakuti iwo akudula tsitsi lawo ndi zinthu."

Ine ndinati, "Zimenezo ndi zolakwika."

Baibulo linati, "Mkazi amene—amene amadula tsitsi lake, mwamuna wake ali ndi ufulu woti amusiye chikwati." Kulondola ndendende. "Iye amachititsa manyazi mutu wake." Ndi zimene Baibulo linanena. Tsopano ine sindikudziwa ngati inu mungazikonde zimenezo kapena ayi, koma ndi zimene Baibulo linanena, mu Akorinto Woyamba.

50 [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]...yogwira thupi mpaka thupilo kumakhala panja. Ndiyeno iwo—iwo amabwerapo, ndikudzati, "Bwanji, Bambo Branham, ndi mtundu wokhawo wa zovala umene iwo akugulitsa."

Iwo akadali nazobe nsalu ndi makina osokera. Palibe chowiringula. Akazi Achiamish ndi Achidunkard akumavalabe zimenezo. Zedi. [Osonkhana akuvomereza—Mkonzi.]

Ndipo chikuchitika ndi chiani? Iwo amapita kunja uko ndipo akumakapitirizabe.

Mkazi anati, "Chabwino, Bambo Branham, ine sindimavala akabudula. Ine ndimavala-..." Ndi chiani zimenezo, ngo ng-...[M'bale akuti, "Ngoleka."—Mkonzi.] Eya. Anati, "Ine ndimavala zimenezo."

Ine ndinati, "Zimenezo ndiye zoipitsitsa." Ine ndinati, "Baibulo linati, 'Ndi themberero kuti mkazi avale chovala choyenera mwamuna.'" Ndipo ndi mawonekedwe owoneka mwamtundu wonyansa bwanji United States alimo tsopano! Mukuona? Kulondola kumeneko.

Mundilole ine ndikuuzeni inu chinachake, mlongo. Inu mukhoza kukhala wangwiro ngati kakombo, kwa mwamuna wanu kapena bwenzi wanu wamwamuna, koma pa Tsiku la Chiweruzo inu mudzakayankha chifukwa chochita chigololo. Yesu anati, "Aliyense amene ayang'ana pa mkazi, namukhumbira iye, wachita naye kale chigololo iyeyo." Ngati wochimwa ameneyo anayang'ana pa inu, ndipo ngati iye ati adzakayankhire pa Tsiku la Chiweruzo. Inu munadzipereka nokha kwa iye. Dzifanizitseni nokha. U-nhu.

Mkazi waumulungu angafunirenji kuti avale monga choncho? Ndiye mukumadzinenera kuti inu muli nawo Mzimu Woyera chifukwa chakuti inu munalankhula mu malirime ndipo munathamanga chokwera-ndi-chotsika? Zimenezo, komanso, ine ndinawawonapo achikunja akuchita zimenezo, Akafula. Mzimu Woyera ndi wangwiro, woyera, wosaipitsidwa. Ndithudi.

51 Bambo uyu anati, "Ngati ndinu...Iwo amakukhulupirirani inu kuti ndi mneneri. Bwanji inu simukuwaphunzitsa iwo momwe angalandirire mpatso zazikulu zauzimu, ndi momwe angamachitire zinthu kwa Mulungu? Bwanji inu simukuwaphunzitsa iwo zimenezo ngati ndinu mneneri?"

Ine ndinati, "Ine ndingawaphunzitse bwanji iwo algebra pamene iwo sakudziwa nkomwe ma ABC awo?" Kodi inu mukudziwa chimene ABC amatanthauza? [Always believe Christ—Wotanthauzira.] Nthawizonse muzikhulupirira Khristu. U-nhu. Inu mungachite motani zimenezo? Mukuona, inu mumafuna kuti mukafike pamwamba apo, mmalo moyambira pansu apa.

52 Mulungu adzamanga Mpingo Wake pa maziko a Yesu Khristu, ndipo limenelo ndi Baibulo. Kunja kwa zimenezo, maziko ena onse ndi mchenga wotitimira. Mulungu samasintha ayi. Chikhalidwe chake sichisintha.

53 Iye anawapanga akazi akhale osiyana ndi mwamuna, ndiponso mwamuna wosiyana ndi akazi. Iye anawaveka iwo mosiyana, ndipo amafuna kuti iwo azikhala mwanjira imeneyo. Mukuona? Akazi akumafuna kuti aziwoneka ngati mwamuna, ndipo mwamuna akumafuna kuti aziwoneka ngati akazi. O, mai! Chisokonezeko chakecho! Ndicho... Ndipo chinthu chonsecho, chikuwoneka ngati chawagwira anthu, ndipo iwe sungathe kuchisintha icho. Chikuwoneka ngati chirombo chachikulu, mdima wawukulu; ngati inu mukumvetsa zimene ine ndikunena, mu mzimu. Chirombo chawagwira iwowo, ndipo iwo—iwo akulephera basi kuti achoke kwa icho; yachuluka kwambiri Hollywood, yachuluka kwambiri televizioni, zachuluka zamkutu zinazo. Chirichonse chimene ife tiri nacho chawonongeka. Nzosadabwitsa, "Ngati ntchitoyo ikanati isafupikitsidwe, chifukwa cha Osankhidwa, sipakanadzakhala mnofu umene uti udzapulumutsidwe."

Inu munati, "Ine sindimazidziwa zimenezo mmbuyomu." Chabwino, tsopano inu mwazidziwa izo, kuyambira pano mpakana mtsogolo. Mukuona? Ndizo...Ine kulibwino ndiimire pamenepo. Tiyeni tibwerere mmbuyo. Zindikirani.

54 Yohane anali chizindikiro. Ndipo kumbukirani kuti, momwe Mulungu anachitira izo nthawi yoyamba, ndi momwe Iye ati adzachitire izo kachiwiri. Iye analonjeza kudzatero. Tsopano, Mulungu sanayambe wawiritsapo ntchito nkomwe gulu la anthu, pa nthawi iliyonse, kwa zoterozo.

Kumbukirani, linalipo gulu nthawi ina, limene, munthu wotchuka dzina lake Ahabu, iye anazipezera... iye anazipezera aneneri achi Israeli foro handiredi. Tsopano, amenewo sanali aneneri achikunja. Aneneri foro handiredi achi Israeli. Iwo onse anali ndi digrii yawo ndi chirichonse, anali ndi sukulu yaikulu.

Kumeneko kunali munthu waumulungu dzina lake Yehosafati, amene anali mfumu ya Yuda, ndipo iye anabwera kumeneko. Ndipo apo ndi pamene wokhulupirira anasakanizikana ndi wosakhulupirira. Zinthu zinalakwika.

Ndipo iye anati, "Ramoti-Giliadi." Tsopano penyani izi, mmene zingakhalire kuti ndi zoono. Iye anati, "Ramoti- Giliadi ndi wa ife, kumeneko. Kumtunda kwa gawo la dziko kumeneko, limenelo ndi lathu." Yoswa, pogawa dzikolo, analipereka ilo kwa Israeli. Ndipo Afilisti, achikunja, anadzabwera ndi kudzawalanda iwo limenelo. Iye anati, "Limenelo ndi lathu."

Tsopano penyani momwe, mwachikhazikitso, anthu angakhoze kukhala kuti akulondola ndipo komabe ndi kuziphonya Izo. Chinthucho ndithudi chinali cha Israeli. Koma malonjezo onse a Mulungu, m'bale, amakhala pa mangawa, mukuona, "Ngati iwo aziyenda kumafika pamaso pa Mulungu."

55 Tsopano taonani apa. Iye anati, "Kodi inu mupita ndi ine, ndi kukandithandiza ine kuti ndilitengenso dziko limenelo? Chabwino, zimenezo, ana Achifilisti awo akudzazitsa mimba zawo kumeneko, ndi tirigu amene ali wa Israeli." Zimenezo ndi zolondola Mwamalemba. Iye anati, "Mundithandize ine kuti ndipite ndipo ndikalitenge ilo."

Anati, "Chabwino, mai..." Pamenepo iye analakwitsa mopupuluma. "Agaleta anga ndi anu, anthu anga ali chimodzimodzi ngati anu. Ine ndipita nawe iwe."

Ndiyeno Yehosafati anayamba kuganiza, inu mukudziwa. "Anati, kodi ife tisafunsire kwa Ambuye za izi ife tisanapiteko?"

"O, zoono," Ahabu anati, "ndithudi. U-nhu. Mundikhululukire ine. I—ine ndimayenera kuti ndiganizire za zimenezo."

"Kodi kulibeko mneneri penapake?"

"O, zedi. Ine ndiri nayo—ine ndiri nayo—seminare ya iwo kumusi kuno, opambana omwe inu munayamba mwawawonapo. Iwo onse amavala zovala zabwino kwambiri. Iwowo ndi masikolala opukutidwa-mwapamwamba kwambiri. Ine ndawaphunzitsa iwo, mpaka pa dontho. Ife tipita tikawatenge iwo."

56 Kotero iwo anapita kumeneko. Ndipo iwo onse anabwera palimodzi. Iwo sanali achinyengo. Iwo anali atapemphera ndi kupemphera, ndi kupemphera mpaka iwo anawona masomphenya.

Ndiye iwo anadzukapo. Ndipo mmodzi wa iwo anadzipangira nyanga ziwiri za chitsulo. Iye anati, "Ndi zimenezi inu mukawakankhira Afilisti, kapena—Asiriya, mukawatulutsa mdzikolo." Iye anati, "PAKUTI ATERO AMBUYE. Pitaniko, Ambuye ali ndi inu." Mmodzi aliyense wa iwo, ndiye, ndi mtima umodzi, anagwera mu mzimu. Aneneri achi Israeli anati, "Pitaniko, Ambuye ali ndi inu." Inu mukuti, kodi zimenezo ndi za Mwamalemba? "Mulungu anapereka cholandira ichi kwa anthu, ndipo mdani anachitenga icho. Inu muli ndi ufulu woti mukachitenge icho."

Tsopano, Achipentekoste, ine ndikufuna kuti inu muphunzire phunziro apa.

Koma, Yehosafati, pokhala kuti ndi munthu waumulungu, iye anati, "Pali chinachake chimene chalakwika pang'ono apa." Anati, "Kodi inu mulibe mmodzi winanso?"

"Mmodzi winanso, pambuyo pa aneneri foro handiredi ophunzitsidwa-bwino akhala apawa?" Ochuluka monga amene akhala pansu apa. "Ataima mu mgwirizano umodzi, akuti, 'PAKUTI ATERO AMBUYE.' Kuchitembenzira icho mmbuyo, ndikuti, 'Yoswa analipereka dzikolo kwa ife. Ilo ndi lathu. Pitani mukalitenge ilo!'"

Koma Yehosafati anafunsa kuti pakhale winanso. Anati, "Kodi palibepo mmodzi wina amene ife tingakafunsire naye kwa Ambuye?"

Iye anati, "O, alipo mmodzi winanso, koma," anati, "Ine ndimadana naye iye." U-hu, u-hu. Anati, "Iyeyo ndi Mikaya, mwana wa Imla." Anati, "Ine ndimadana naye iye. Iye nthawizonse amakhala akunena zinthu zoipa za ine."

Anati, "Musalole kuti mfumu inene chomwecho. Pitani mukamutenge iye."

57 Ndiye iwo anatomizako othamanga ena kumeneko. Ndipo ena a iwo anati, "Tsopano, Mikaya, ine ndikufuna kuti ndikuuze iwe chinachake. Tsopano, iwe ukudziwa kuti iwo anakuchotsa iwe, anakuchotsa iwe mu chiyanjano, osati pakale, chifukwa iwe nthawizonse umakhala ukunena zinthu zoipa kwa anthu. Tsopano ngati iwe ukufuna kuti akubwezere khadi lako la chiyanjano, iwe ukanene chinthu chomwecho chimene iwo akunena, ndipo, o, iwo akangokutengera iwe basi mu nkhwapa mwawo."

Koma iye anapezeka kuti iye anali mneneri weniweni. Iye anati, "Pali Ambuye Mulungu, ine ndingonena chimene Mulungu ayika mkamwa mwanga." O! Mulungu amudalitse munthuyo. Iye anati, "Mudikire mpaka usikuuno, ndipo ine ndiwona zimene Ambuye andiuze ine."

Mmawa wotsatira, anati, "Pitani kumeneko, koma ine ndinawona Israeli atabalalika ngati nkhoa zopanda m'busa." Ndiye iye anatenga masomphenya ake ndi kuwafanizitsa iwo ndi zimene Eliya ananena, chimene chinali chitachitika kwa Ahabu. Iye akanakhoza bwanji kudalitsa zimene zinali zitatembereredwa? Zinalibe kanthu kuti anali ochuluka bwanji...

58 Iye ndi fuko laumulungu. Mpingo wa Chipentekoste, Abaptisti, ndi Amethodisti, ndi ena otero, ali mpingo wa Chikhristu, koma inu mungathe bwanji kudalitsa chimene Mulungu wachitemberera? Ine sindikusamala, inu mukuti, "I—ine ndinajowina ichi. Ine ndinachita ichi." Chimenecho chiribe kanthu kochita nazo izo. Taonani zimene inu mwachita. Tayang'anani pa Achipentekoste, momwe iwo alekererera zigwiriro. Taonani zomwe inu munalu, ndipo muwone zomwe inu muli tsopano. Nzosadabwitsa, maso ali, maso achititsidwa khungu.

59 Ndiye iye, Ahabu, a...Wansembe uyu anamuwomba khofi iye pa kamwa. Ndipo anati, "Kamuikeni iye," ndipo Ahabu anati, "kamuikeninso iye uko mndende ya mkati. Ine ndikadzabwerera mu mtendere, ine ndidzathana naye munthu ameneyu."

Iye anati, "Ngati inu muti mudzabwerere nkomwe, Mulungu sanalankhule ndi ine." U-hu? Mukuona? Apo panali mneneri, apo panali chizindikiro; apo panali liwu Lake. Ndipo, kulephera kulimvera ilo, kunabweretsa chiweruzo.

Mzimu Woyera ndi mneneri wathu lero. Kodi mulephera kuti mumvere Liwu Lake? Iye akuzindikiritsidwa mu Lemba, kuti Iye akanadzanena zinthu zimenezi. Yesu Khristu, mawonekedwe a Mzimu Woyera!

60 Mulungu anachita ndi munthu mmodzi uyu. Uyu, Mulungu samachita konse ndi magulu; amachita ndi munthu mmodzi. Eliya sanali gulu. Yohane sanali gulu. Iwo sanali gulu kapena chipembedzo, osati aliyense wa iwo. Koma onsewo ankatsutsa zoterozo. Uko ndi kulondola. Yohane anati, "Musamaganizire zomanena kuti ife tiri naye Abrahamu ngati atate wathu. Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana kwa Abrahamu."

Ndipo chizindikiro cha nthawi-yomaliza chidzakhala ndi Liwu la nthawi-yomaliza. Ndipo chizindikiro cha nthawi-yomaliza chidzakhala molingana ndi zimene zinanenedweratu mu Baibulo. Ndipo Liwu la nthawi-yomaliza, limene likutsatira chizindikiro cha nthawi-yomaliza, lidzazindikiritsidwa ndendende mu Lemba, lidzakhala Lemba limene linalonjezedwa.

Tsopano ife timawerenga mu Luka 17 chimene chizindikiro cha nthawi-yomaliza chiti chidzakhale, zidzakhala monga zinali ku Sodomu, lonjezo. Ndipo ife tiri naye Sodomu mwachithupithupi, nanga bwanji ife sitikuhulupirira chizindikiro mwauzimu apa? Ngati inu mungathe kuwawona Malemba, apanso, Luka 17 ndi chizindikiro, ndipo Malaki

ndi Liwu. Chizindikiro chinali ngati kuti Mulungu akuwonetseredwa mu thupi, kumadziwa zobisika za mu mtima; ndipo Liwu la Malaki 4 linali kuwatembuzira anthu achoke kwa tizikhulupiriro tawo, abwerere ku Chikhulupiriro cha atate. Chimenecho ndiye chizindikiro.

61 Inu mukudziwa chiani? Ine ndikutseka tsopano. Zizindikiro kawirikawiri zimalandiridwa, zedi; koma, liwu, o, ayi. Liwu limene limatsatira chizindikiro, iwo samafuna kalikonse kochita ndi zimenezo. Inde.

Chizindikiro cha Yesu, ngati Mesiya, kudzachiritsa odwala, iwo anavomereza zimenezo. Koma tsiku lina Iye anati, "Ine ndi Atate ndife Amodzi."

O, mai, liwu limenelo silinalandiridwe. Iwo anati, "Inu mumadzipanga Nokha Mulungu, wofanana ndi Mulungu."

Iye anati, "Ine ndine Mwana wa Mulungu."

"O, mai, zingatheke bwanji kuti Mulungu akhale ndi Mwana? Mwaona, sizingatheke kuti Mulungu akhale ndi Mwana!"

Koma, inu mukuona, iwo anachikhulupirira—chizindikiro, odwala amakhoza kuchiritsidwa, ndipo, o, zimenezo zinali zodabwitsa, zimenezo zinali zokoma basi. Koma pamene zinafika ku liwu, iwo sanafune kuti alikhulupirire liwu. Kodi iwo anachita chiani? Iwo anamuika Iye panja.

Ndipo kodi inu mukudziwa chiani? Baibulo limatiuza ife, mu Chivumbulutso mutu wa 3, pa M'badwo wa Laodikaya uwu, kuti Iye akanadzachitidwa chinthu chomwecho. Iye anali kunja kwa mpingo. Amenewo ndi Mawu akuwonetseredwa. Iye anali Mawu akuwonetseredwa. Iye panobe adakali Mawu akuwonetseredwa.

62 Ngati inu mungathe kukhulupirira chizindikiro cha Sodomu, cha Luka, ngati inu mungathe kukhulupirira zimenezo, ndiye bwanji simukuvomereza Liwu la Malaki 4? Mukuona, bwanji osati inuyo, inu? Izo zikhoza kuvomerezedwa. Njira yokha yomwe izo zingachitidwe ndi... Chizindikiro chikhoza kutsimikiziridwa, koma inu muyenera kuvomereza Liwu.

Mose anatumidwa kuti apite kumeneko, mwa thupi, ndipo akatenge chizindikiro chazimu ndipo akawaitanire anthuwo kubwerera ku lonjezo la makolo.

Malaki 4 ali woti adzawabwezeretse anthu "Kubwerera ku Chikhulupiriro cha atate." O, bwererani, O akhungu ndi omwazika, komwe kuli kwanu!

63 Potseka, ine ndinena izi, ndemanga yotsiriza iyi. Mneneri anati, "Kudzakhala Kuwala mu nthawi yakumadzulo." Taonani, iye anati, "Lidzakhhalapo tsiku limene silimadzatchedwa masana kapena usiku." Tsopano mvetserani. Ine ndikutseka. "Lidzakhhalapo tsiku..." Mulole izi zilowe mwakuya, ndipo Mulungu ataziya izo mu mtima uliwonse mu gulu ili, usikuuno, mu nyumba yolankhuliramo ino. Mneneri anati, "Lidzakhhalapo tsiku limene silimadzatchedwa usana kapena usiku, lokhala ngati lachimbuuzi, lamvula, tsiku lachifunga. Koma," anati, "pa nthawi yamadzulo, padzakhala Kuwala."

Tsopano, kumbukirani, dzuwa nthawizonse limatulukira Kummawa ndipo limapita kumadzulo. Chitukuko chalitsatira dzuwa. Inu mukudziwa zimenezo. Ndipo, zindikirani, dzuwa lomwelo limene limatuluka Kummawa ndi dzuwa lomwelo limene limakalowa Kumadzulo. Tsopano, chitukuko chayenda ndendende limodzi ndi dzuwa, mpaka tsopano Kummawa ndi Kumadzulo zakomana. Ife tiri pa Gombe la Kumadzulo; Kummawa ndi Kumadzulo.

Ndipo, kumbukirani, Uthenga wayenda njira yomweyo. Iwo unatulukira Kummawa, kubwera kwa Yesu Khristu, M-w-a-n-a, osati d-z-u-w-a. M-w-a-n-a, Mwana wa Mulungu, anawuka Kummawa, kwa anthu aku Mmawa.

Ndipo tsopano lakhalapo tsiku limene anthu ajowina tchalitchi, apanga zipembedzo, kuwala kokwanira basi kuti aziwona, "Chabwino, ife tikhala ndi tchalitchi. Ife timanga ichi. Ife timanga sukulu. Ife timanga chipatala. Ife tiwaphunzitsa. Ife tikhala ndi seminare." Iwo akhala nako kuwala kokwanira kuti achite zimenezo.

64 Koma, kumbukirani, Baibulo linati, mneneri wa Ambuye, mu Baibulo, amene ali PAKUTI ATERO AMBUYE, "Dzuwa lomwe lija limene linawalira Kummawa lidzawalanso kachiwiri Kumadzulo, pa nthawi ya kumadzulo. Kudzakhala Kuwala mu nthawi ya kumadzulo."

65 Kodi Iye adzachita chiani? Adzachita ndendende zomwe zija zimene Iye ananena mu Luka mutu wa 17. "Pa nthawi yomaliza, pamene Mwana wa munthu akuwululidwa mwanjira yomweyo yomwe Iye anali Kummawa, Mwana yemweyo akuwala, Mphamvu yomweyo, Mzimu Woyera womwewo, Chinthu chomwecho chikuchita chinthu chofanana. Kudzakhala Kuwala mu nthawi yakumadzulo."

Dzuwa lomwelo limene layenda; M-w-a-n-a yemweyo amene wayenda; wabwera kudutsa Kummawa, kuchokera kwa Paulo; analumphira mpaka ku Germany, pa Marteni Lutera; analumpha kachiwirinso, pa chikoka Chake chotsatira; ndipo anapita kuchokera pamenepo mpaka ku England, kwa John Wesley; analumpha kudutsa Nyanja ya Atlantic, mpaka ku United States, kwa Achipentekoste; ndipo tsopano Chipentekoste chadzitsitsa chokha, ndipo ife tiri pa Gombe.

Mmodzi aliyense wa iwo, anachita chipembedzo, chimodzimodzi monga iwo anachita pachiyambi, anapanga bungwe limene Mulungu analitemberera. Chipentekoste, ndi zonse, zinachita zimenezo.

66 Koma Iye anati, "Kudzakhala Kuwala mu nthawi ya kumadzulo. Padzakhala chizindikiro chiti chidzauke mu nthawi ya kumadzulo." Musachiphonye Ichi, abwenzi. Musachiphonye Ichi. Tsopano, Mwana yemweyo adzapereka Kuwala komweko. D-z-u-w-a lomwelo likupereka kuwala kwa d-z-u-w-a komweko. M-w-a-n-a yemweyo akupereka Kuwala kwa M-w-a-n-a komweko.

Tsopano, amenewo si maneno anga. Aliyense pano, amene akudziwa kuti Baibulo limanena zimenezo, kwezani manja anu. [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Ndizo ndendende zooni.

Tsopano, inu mukhoza, izo ziri ndi inu. Mukhulupirire kuti Mwana wa Mulungu, Yesu Khristu, ali, sali wakufa. Iye ali wamoyo. Iye ali mu kudzichepetsa, kudzichepetsa. Iye nthawizonse ankakhala monga choncho. Njira yopitira mmwamba ndiyo kudzitsitsa. Muzidzichepetsa nokha, muchokeko ku malingaliro anu okhuthara, ndipo mumkhulupirire Ambuye Yesu. Muziwona chizindikiro, ndiye muzikhulupirira Liwu. Bwererani, O omwazika, komwe kuli kwanu!

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu.

“Ndipo ngati iwo sakakhulupirira Liwu la chizindikiro choyamba, mdzanja, monga izo zinali ndi Mose, ndiye ukachite chizindikiro chachiwiricho. Ndiye, ngati iwo sakakhulupirira chizindikiro ichi, ndiye ukatenge madzi (madzi amaimira moyo) mmenemo ndi mnyanja ya mchere kapena mnyanja, ukawatsanulire iwo pansu, iwo akasanduka magari.”

67 Atate akumwamba, ndi mochedwa kwenikweni tsopano, koma Inu munalonjeza kuti padzakhala Kuwala kumadzulo. Mulole Liwu la Uthenga wathu lilowerere mwakuya mu mitima ya anthu, pamene iwo akusinkhasinkha pa Iwo ndi kuphunzira izo mwa Mawu.

Muwadalitse amene akukhala kuno, Ambuye. Muwadalitse anthu awa. Mwawawona iwo akhala apa, anjala, ana osauka akukankhidwa-kankhidwa ndi kumapondedwa, ndi ichi, tikudziwa kuti Satana anachita zimenezo kuti angowapangitsa iwo khungu kwa chinthucho pamene Icho chizifika pamenepo. Mulole iwo, usikuuno, ndi mtima umodzi, amukhulupirire Yesu Khristu, akhulupirire lonjezo Lake, kuti Iye wauka kwa akufa.

Inu munati, “Mu nthawi imene iwo sakuiganizira, ndiye Mwana wa munthu adzabwera.”

Panthawi imene mpingo wapeza zake, uli ndi ndalama zambiri, ukumanga mamiloni a madola mu zinyumba. Iwo angakhale pabwinoko, Atate, ine ndikukhulupirira, atakhala kumbuyo uko ataima pa ngodya, akuimba—nkhotcho, ali ndi chipewa mdzanja lawo, ng'oma yakale ili pa ngodya ngati a Salvation Army, kuposa momwe zikanakhalira kukakhala mosungira mitembo umu usikuuno, kuyesera kuti afanane ndi dziko lapansi, “Okhala nawo mawonekedwe aumulungu, ndipo ndi kumakana Mphamvu yake.”

Perekani, Ambuye, usikuuno, kamodzinso, Ambuye; monga Samson anafuula, “Kamodzinso, Ambuye, kamodzinso.” Mulole zidziwike kuti Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu; yemweyo dzulo, lero ndi kwanthawizonse. Ndipo muzidzindikiritse Nokha pakati pathu, kuti iwo akhoze kuwona chizindikiro, mwinamwake iwo akhulupirira Liwu. Mu izi, ine ndikupempha mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

68 Ife tiyitanira mzere wa pemphero, mofulumira ndithu. Ine ndawona kuti nthawi yake yeniyeni ndi ino pakali pano imene ife tikanamabalalika. Koma tiyeni tikhale ndi mzere wa pemphero, basi mzere wa pemphero waung'ono, ndiye tidzayambira mawa.

Iye anapereka makadi a pemphero lero. Choncho, ife tikumapereka makadi tsiku lililonse, kuti wina aliyense akhoze kupeza mwayi wobweramo, nthawi yodabwitsa. Kufika mu mzere wa pemphero, zimenezo sizimakuchiritsani inu. Aliyense akudziwa, mu msonkhano uliwonse, amakhalapo ochuluka amene amachiritsidwa kunja uko kuposa amene amachiritsidwa kuno, mwaona, nthawizonse. Mzimu Woyera ndi wopezeka ponseponse basi. Iye akungoyesera kuti awapeze okhulupirira, ndi zokhazo, Iye angakhoze kuwafikira.

69 Anapereka makadi a pemphero P, monga Paulo. Tiyeni, takhala tiri pati...Chabwino, nditana kuyambira wani. Wani, thuu, firii, foro, faifi, sikisi, seveni, eyiti, naini, teni, asiyeni iwo aimirire cha apa, ngati inu mungathe. Khadi lawo la pemphero P, monga Paulo, wani mpaka teni, muimirire cha apa mbali iyi, ngati inu mungathe kuimirira. Ngati inu simungathe, ndiye ife tipeza wina kuti akuthandizeni inu. Teni; wani, thuu, firii, foro, faifi, sikisi, seveni, eyiti... Chabwino, awiri enanso. Eyiti, naini, teni, chabwino. Teni mpaka fifitini, teni mpaka fifitini, amenewo ndi asanu enanso. Fifitini mpaka twente, taimirirani kuti ine ndikuwoneni ngati inu mukuimirira; P, fifitini mpaka twente. Twente mpaka twente faifi. Tiyeni tiwone tsopano, paliponse pamene inu muli. Tsopano omvetsera onse akhale molemekeza kwenikweni, maminiti pang'ono okha. Imeneyo ikhala khadi la pemphero P, wani mpaka twente-faifi. Sichoncho izo? Twente-faifi, wani mpaka twente-faifi.

70 Tsopano wina aliyenseyo mukhale molemekeza kwenikweni. Mumupatse Mulungu ulemu wochuluka chomwecho, apereke Uthenga. Inu muli angongole kwa Mulungu, kuti mupenyetsetse miniti ndi kulingalirapo.

Tsopano ine ndikuganiza iwo akuwakonzekeretsa anthuwo. Iwo amene sangathe...Ngati iwo ali ndi khadi la pemphero, iwo onse sanakhale pa mzere, iwo akafufuza; iwo andiiza ine mu maminiti pang'ono, ndiyeno iwo adza...ndiye ife tiwona ngati winawake ali wogontha kapena winawake amene sangathe.

Ine sindikudziwa pamene iwo ali, abwenzi, makadi a pemphero amenewo. Mnyamata amabwera kuno...[M'bale Branham akumufunsa winawake pa nsanja, “Ndani anapereka iwo? Kodi ndi inuyo, kapena Billy? Billy?”—Mkonzi.] Pamene iye abwera kuno, ndipo amadzawasakaniza makadi amenewo, pamaso pa anthu inu, ndiye amakupatsani inu khadi la pemphero; amabwera komwe kuno, ndikudzakuuzani inu nonse kuti mukhale pansu, amakupatsani inu khadi la pemphero. Mukuona? Ine sindimadziwa kuti iwo akhala pati. Ine ndakhala ndikuyesera kuti ndimufikitse mwana uyu pano, mukuona. Ndi, ena, i—ine sindikukudziwani, i—ine ndiribe njira yoti ndingadziwire zimenezo. Ine ndikuganiza Mulungu amangozidzoza izo mwanjira yomwe Iye akufunira kuti izo zidzozedwere monga choncho.

71 Tsopano, tsopano nonse a inu, amene mulibe khadi la pemphero. Mukwezere mmwamba dzanja lanu, ndikuti, "Ine ndiribe khadi la pemphero, koma ine ndikudwala." Kwezerani mmwamba dzanja lanu, paliponse mnyumbayi. Ine sindikusamala kuti inu muli pati, kwezerani mmwamba lanulo...Chabwino, palibepo anthu ambiri pano ndiye, tsopano. Chabwino, molingana ndi zimenezo, izo sizitenga nthawi yaitali kuti tipempherere mzere wa pemphero tsopano mawa. Alipo pafupifupi twente ali muno, kupatula amene aimirira muno, amene akudwala.

Zimenezo ndi zabwino. Ndine wokondwa kukuwonani inu mukulandira zimenezo monga choncho. Inu munali ndi chikhulupiriro chochuluka kuposa momwe ine ndimaganizira kuti inu munali nacho, mwinamwake. Mukuona? Mukuona? Ngati inu mwavomereza machiritso anu, itayeni khadi yanu, Mulungu akudalitseni inu. Chimenecho ndicho chikhulupiriro chenicheni choona. Palibe amene anadzaika manja pa inu; inu munaika manja pa Khristu.

Tsopano inu pano usikuuno, amene simukhala mu mzere wa pemphero, inu muikhulupirira nkhani iyi. Monga mkazi amene anakhudza mphonje ya chovala Chake, ndipo Iye anapotoloka ndipo anazindikira kuti iye anamukhudza Iye, ndi angati akuikumbukira nkhaniyo? Zedi, inu mukutero.

Tsopano kodi inu mukukhulupirira zimenezo, Iye, Baibulo linanena mu Ahebri 4, kuti, "Iye ndi Wansembe Wamkulu, pakali pano, amene angakhoze kukhudzidwa ndi zomverera za zifooko zathu?" [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Chabwino, ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, kodi Iye sangachite chimodzimidzi? ["Ameni."] Kodi Iye sanazichite zimenezo, usiku ndi usiku, pano? ["Ameni."] Ndi angati amene anakhalapo mu misonkhano ina ndipo anamuwonapo Iye akuchita zimenezo? Ingokwezani. ["Ameni."] Zedi. Mukuona? Kuzungulira dziko! Iye akudziwa, Iye amadziwa zonse za inu.

72 Tsopano taonani zimene ine ndikuyesera kuti ndichite. Ndi angati akumvetsa zimene ine ndikufuna kuti inu muchite? Mukuona? Ine ndikufuna inu, popanda aliyense kuti ayike manja pa inu, ine ndikufuna inu, ngati chida chenicheni cha Mulungu, munene kuti, "Yesu Khristu, ine ndikukukhulupirirani Inu. Ine tsopano ndikukulandirani Inu ngati mchiritso wanga. Ine tsopano ndikukulandirani Inu ngati Mpulumutsi wanga. Ine ndikukhulupirira izo ndi mtima wanga wonse, ntchito yake yagwirika." Ndiye mugwiritse lonjezo limenelo, mugwiritse kuvomereza kwanu ndipo muziyenda chitsogolo ndi izo. Muwone zimene zitachitike. Mukuona? Muwone zimene zitachitike. Mukuona? Tsopano ndi zimene ine ndikuyesera kuti ndikufikitseni inu pozichita, njira yeniyeni imene ife tikuyenera kumakhulupirira.

Kodi inu mukuti chiani? [Winawake akuti, "Foro ndi naintini."—Mkonzi.] Nambala foro, khadi la pemphero nambala foro ndi nambala naintini, akusowa. Khadi la pemphero foro. Muyang'ane pa winayo; muyang'ane pa khadi la woyandikana naye wanu. Khadi la pemphero nambala foro ndi nambala naintini. Chabwino, mphindi chabe, dikirani. Tiwone, ngati ine sindimuitana iye, ndiye kuti ine sindikumveka pa zimenezo, inu mukuona. Mukuti chiani? Mukuti chiani? ["Foro."] Mwaipeza foro? Nanga bwanji naini... Simunaipezebe naintini. Mukuti chiani? ["Kuphatikizanso foro."] Khadi la pemphero foro silinapezekebe, kapena naintini. Ngati winawake ali ndi makadi amenewo, ngati inu mungabwere pa mzere. Kapena, taonani, tiwone, iyo ikhoza...alipo aliyense... Kodi mwana wamng'ono uyo ali ndi khadi? Tafufuzani, si imeneyo...Nambala yake si imeneyo. Kodi dona uyu apa ali ndi khadi, mu chikuku ichi? Tafufuzani nambala yake. Kodi imeneyo—imeneyo ndi nambala yake? Dona ali pa machira, nhu? Iwo aipeza iyo. Iwo, onse abwera tsopano. Zabwino. Chabwino. Tsopano—tsopano, anthu inu amene muli ndi khadi la pemphero, agwirizitseni iwo. Ife titumikira, mwa chisomo cha Mulungu.

73 Tsopano, abwenzi, uno pokhala usiku womaliza umene ife titi tikhale nawo, mawa ndi Lamlungu madzulo, tiyeni tidzikhalitse chete. Tsopano mungotenga kusakhulupirira konse kumene inu muli nako ndi —lingaliro losakhulupirira konse, ndipo muligoneke ilo pansu, ndipo mupondetsepo phazi lanu pa ilo, monga izo zinali. Ndikuti, "Ambuye Yesu, ine ndikukhulupirirani Inu." Ndi angati amene ati achite zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Zikomo inu. Mulungu akudalitseni inu.

Tsopano asachokepo wina aliyense. Mungokhala mwabata kwenikweni, ndipo muzikhulupirira. Tawonani mbali iyi, ndipo tsopano tayang'anani.

Kuzindikiritsidwa kwa Mulungu nthawizonse kwakhala kuli kudziwa, kukhoza kuwoneratu zomwe zakhala ziripo, ndi kunena zomwe zakhala ziripo, zimenezo zimakhala chotani, kapena padzakhala chiani. Ife tikuzidziwa zimenezo. Umo ndi momwe aneneri ankadziwidwira. Umo ndi momwe Yesu anadziwidwira kuti ndi Mesiya. Ndipo Iye ndi Mesiya yemweyo lero monga Iye anali nthawi ijayi, kokha kuti alibe thupi logwirika kuno pa dziko lapansi. Iye anawutumizanso Mzimu Wake kuti uzidzagwiritsa ntchito thupi lanu, thupi langa. Tsopano, inu mwina simungathe kuchita izi. Ife tikudziwa, mu Lemba, amakhalapo mmodzi mu kam'badwo. Koma, mukuona, komabe inu mukhoza kukhulupirira zimenezo, ndipo inu muli ndi zinthu zina zimene inu mungathe kuchita, aliyense.

Nanga bwanji ngati chala changa chitasankha, chifukwa icho si diso langa, kuti icho sichikhalanso chala changa? Nanga bwanji ngati nkono uwu utati, "Ine sindimakwezanso mmwamba kenanso, chifukwa ngati ine si diso, kapena khutu, ine sindikhala nkono?" Bwanji, izo zingapundule thupi langa.

Inu muzikhala chimene Mulungu anakuikani inu kuti mudzakhale.

74 Kodi ndi nthawi zingati ine ndamuyamikirapo Oral Roberts, Billy Graham, Tommy Osborn!

Ena a amuna amenewo amayenda pamenepo ndikuti, "Ulemerero kwa Mulungu! Mukhulupirire zimenezo!" Chikhulupiriro cha Galuwamkulu. Ndi kuchokapo, kuchoka pamenepo ali osatopa basi monga mmene iwo akadakhala.

Billy Granham akaima ndi uthenga, ndi kulankhula ndi anthuwo maminiti pang'ono, amati, "Pangani chisankho chanu; bwerani ku guwa." Mungoima pamenepo, musapange kusuntha kwina.

Iye anati, "Ndiye nchifukwa chiani iwe umachita zimenezo, Billy?"

Anati, "Uthenga wanga unalalikidwa. Iwo unachokera kwa Mulungu." Ndiko kulondola.

Iye ali ku mpingo waku Sodomu uja, basi ndendende zimene ziyenera kukhala. Dzina lake lothera ndi h-a-m kuchokera kwa Abraham, zilembo sikisi; Abraham anali seveni. Mukumuona mtumiki wa mpingo umenewo, akutsikira uko ku Babeloni? Ndithudi. Palibepo munthu mu dziko amene ali ndi uthenga uwo wa kulapa, monga Billy Graham. Iye amaima pamenepo. Amachoka pamenepo, ndi kupita kukadya nyama ya T-boni ndi kupita kukagona, kukamwa mkaka wosungunulidwa. Zimenezo ndi zabwino.

75 Ndipo pamene iwe uyenera kuti uyime ndi kumenyana ndi ziwanda! Nthawi ina ku Long Beach, M'bale Jack ndi ine... Abambo anu anali ataima pamenepo.

Ndipo apo panaima Bambo Fuller, Charles Fuller, m'bale wabwino, anaima pamenepo akulalikira. Pafupifupi anthu masauzande awiri kapena atatu pamenepo madzulo amenewo. Iye tinakhala ndi kumamvetsera pa msonkhano wake. Ine ndinali nditabwereka nyumba yolankhuliramoyo, atatha iyeyo. Ndipo iye anaima pamenepo ndipo analankhula bwino. Ndipo anati, "Aliyense muno amene akufuna kuti amulandire Khristu?" Anthu awiri kapena atatu anabwera kuti adzadalitsitse ana awo. Mkazi mmodzi anati amafuna kuti avomereze zimenezo. Anabwerapo ndipo anapemphera pemphero lapang'ono, mmodzi wa madikoni, anabwerera ndi kukakhala pansu. Anagwirana manja, anapotoloka ndi kumatulukapo. Apo panali gulu lake laluntha, lovekedwa- bwino la anthu, likutuluka pamenepo.

Apa panabwera anga, mmachira, zikuku, akhungu, olumala, osayenda, ovulazidwa. Pamene chikhulupiriro chako chiyang'anizana ndi chinachake chonga zimenezo!

Tsopano apa, kodi ine ndadzinenera kuti Khristu ndi chiyani? Ndipo tsopano osakhulupirira atakhala pomwepo, akufunafuna kuti apeze cholakwika chimodzi, mukuona, basi akungoyesera kuti apeze cholakwika chimodzi.

76 Ndikukumbukira, kuno osati kale litali ku Toronto, ife tinali titaima pamenepo ndikulalikira, ndikupempherera odwala. Ine ndinakhala ndikumverera mzimu wachirendo; iwo unali utakhala cha kumamzere kwanga. Ine ndinakhala ndikuwuyang'anitsitsa iwo. Apo panali bambo atakhala pamenepo, gulu linali litamuchita ganyu iyeyo kuti abwere adzandipepetule ine. Iye amakhoza kupita kukazungulira kwa misasa ya asilikari ndi kuwapangitsa asilikariwo kumayenda ndi manja awo ndi kumakuwa ngati agalu, ndi zinthu; kumawapepetula. Ine ndinaumverera mzimu woyipa umenewo. Ine sindimadziwa kumene iwo unali kuchokerako. Ine ndinakhala ndikuyang'anitsitsa. Ine ndinawuwona mthunzi wakuda umenewo. Ine ndinadikirira maminiti pang'ono chabe. Ine ndinati, "Iwe mwana wa Satana, chifukwa chiani mdierekezi wachititsa khungu malingaliro ako kwa chinachake chonga chimenecho? Chifukwa chakuti iwe wabwera kuti udzapikitsane ndi Mulungu, kudzawutsutsa Mzimu wa Mulungu, iwo achita kukunyamula iwe pano." Iye anapuwala pomwepo pamene iye anakhala ndipo akadali chipuwalirebe. Mukuona?

77 Ife sitimachita masanje a tchalitchi. Ndi angati amene anayamba akhalapo mu misonkhano ndipo anawonapo zinthu zofanana ndi zimenezo zikuchitika, inu mukudziwa zinthu zimene zimachitika? Zedi. Ndizoona. Kumbukirani, mukhale—mukhale molemekeza.

Tsopano apa pali, ine ndikuganiza, munthu woyamba. Ndi kulondola kumeneko?

Tsopano, mukuona, ine ndalalikira, ndakuuzanipo inu ndendende zimene zimayenera kuti zichitika mu tsiku la lero. Tsopano zimenezo ndi chizindikiro, ngati izo zichitika. Ndi chimene chizindikiro chinali, ndiye mukhulupirire Liwu limene likutsatira chizindikirocho. Mukuona?

Tsopano apa pali mkazi. Ndendende, kwa inu obwera atsopano, uyu ndi Yohane Woyera 4, pamene Ambuye Yesu wathu anakomana ndi mkazi pa chitsime. Iwo anali asanayambe akomanapo, mmoyo, ndipo Iye anamuza mkaziyo limene linali vuto lake. Ndipo iye anazindikira kuti ameneyo anali Mesiya. Inu mukuidziwa nkhanayo? Ndi izi pano kachiwiri, mwamuna ndi mkazi akomana. Tsopano iyeyo sikuti ndi mkaziyo, ndipo sindine Mwamuna ameneyo, koma zimenezi ndi Mulungu yemwe uja. Mukuona? Tsopano, Yesu anati, "Ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso muzidzazichita," Yohane Woyera 14:12.

78 Tsopano, dona, sindikukudziwani inu, sindikudziwa chimene inu mwaimira pamenepo. Ilo likhoza

kukhala vuto la pakhomu. Mwina izo zikhoza kukhala za winawake. Mwinamwake inu mukudwala. Mwinamwake ndi... Mwinamwake inu mukuima pamenepo, mwangozivekapo chinachake. Ngati izo ziri, mungofufuza zimene zingachitike. Mukuona? Mwinamwake inu mukutsanzira chinachake. Chirichonse chimene icho chiri, ine sindiri...Inu mukhoza kukhala wokhulupirira weniweni. Zimenezo ine sindikudziwa, koma Mulungu akudziwa. Koma inu mudziwa ngati Iye wakuwuzani inu zoono kapena ayi, sichoncho inu? Ngati izo ziri zoono, inu mudziwa zimenezo.

Tsopano, taonani, ndicho chimene chikhulupiriro chanu chiyenera kuchita. Inu mukufuna mubwere chotani kuno? Tsopano ngati aliyense akukhulupirira kuti ndi zolakwika, inu mubwere kuno ndipo mudzamutenge wodwala uyu, mubwere kuno ndi kudzawatenga ena onsewa. Ndiye ngati inu simungachite zimenezo, ndiye musandiweruze ine. Mukuona?

Tsopano taonani apa, mlongo, miniti yokha. Tsopano ine ndiribe lingaliro, ndiribe kanthu ka inu. Inu mwangokhala mkazi mwaima pamenepo.

79 Tsopano ngati Ambuye Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, Amene ine ndamutsimikizira mwa Baibulo, analonjeza kuti Iye akanadzabwerera mu masiku otsiriza ndi kudzaziulula Iyeyekha mu chidzalo cha Mzimu Wake.

Chimodzimodzi ngati Mpingo ukukwera mmwamba; monga momwe zimabwerera kwa munthu, njira yonse kuyambira ku mapazi, kukwera mmwamba mu ntchafu, mpaka ku mutu, ndipo mutu ndiye mutu wa thupi. Ndipo Thupi labwera mmwamba, kuyambira pa Mpingo woyamba, wakhala ukubwera chokwera, mu ichi, mu kukonzanso, wakhala ukukwera mpaka pakali pano. Iwo wabwera kudutsa mu kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera. Tsopano ndi Mutu (Khristu) kumabwera ku Thupi, Thupi la Khristu. Iyeyo ndi Mmodzi Amene akudziwa. Dzanja langa silimadziwa kuchita, basi limangodalira mutu wanga. Koma Iyeyo ndi Mmodzi Amene amadziwa, ndicho chifukwa chake Iyeyo ali Mawu.

Ine sindine Mawu. Ine ndine munthu. Koma, inu mukuona, Iye amagwiritsa ntchito thupi ili. Chifukwa, Iye anafa kuti adzaliyeretse thupi ili, kuti Iye adzakhoze kuligwiritsa ilo ntchito, ndi kudzapereka mphatso. Basi kukhala ngati kulichotsa ilo mu giyala, kenako Mzimu Woyera nkudzapitiriza.

Ndiye, ngati Iye angafotokoze kapena kukuuzani inu zimene inu mwazichita, chimene inu mwadzera pano, kapena chinachake chokhudza inu, inu mukhulupirira izo. Ndipo omvetsera akhulupirira chomwecho? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Mulole Ambuye Mulungu apereke izi.

80 Tsopano ine ndikuwutenga mzimu uliwonse, muno, pansu pa ulamuliro wanga, kwa ulemerero wa Mulungu. Tsopano mukhale bata. Musayendeyende.

Taonani kuno, mphindi yokha. "Tandiyang'anani ine," monga Petro ndi Yohane ananena, akudutsa pa chipata. Mwakulankhula kwina, mungokhala ndi tcheru kwa zimene ine ndikulankhula. Mukuona?

Yesu anamufunsa mkaziyo mafunso pang'ono. "Undibweretsere Ine akumwa."

Mukuona, ine ndakhala ndikulalikira, chinthu chomwecho. Atate anandituma ine kuno ku—ku Baton Rouge. Ine ndiri kuno.

Atate anati Iwo ankafuna kuti adzere ku Samaria. Iye anakhala pamenepo. Mkazi anali woyamba amene anafika kwa Iye. Iye anachita chizindikiro chimodzi chimenecho pa mkazi ameneyo, ndipo mzinda wonsewo unalapa. Ndi kusiyanita bwanji komwe...

81 Inu mukuganiza, ngati Iye angachite chinthu chomwecho, usikuuno, inu mukuganiza kuti onse aku Baton Rouge angalape? Ine ndikukaikira zimenezo, sichoncho inu? Ine ndithudi ndikutero. Koma ife tiri mu masiku otsiriza, pamene choipa chiri choipa kwambiri kuposa momwe zinayamba zadziwidwirapo.

Tsopano zosowa zanu. Inu muli pano kuti mudzapemphereredwe. Kulondola ndendende. Ndipo inu mukuvutika ndi vuto la kumero. Ngati zimenezo ziri zoono, kwezani mmwamba dzanja lanu. Si zokhazo ayi, koma pali winawake amene inu mukumupempherera. Ndi mwana, ndipo mwana ameneyo ali ndi vuto la kumero. Ndipo ndi vuto la kumero kwa mwanayo, pali zomera pa mmeropo. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu amuchiritsa iye, nayenso? Mpango uwo umene uli mdzanja lanu, umene inu mwawukwezera kwa Mulungu, ngati umboni. Musakaikire zimenezo tsopano. Mupite ndipo mukawuike mpangowo pa mwanayo. Musakaikire, ndi mtima wanu wonse. Mulungu akuchiritsani nonse a inu ndipo akupangani inu abwino. [Mlongoyo akuti, "Alemekezeke Iye! Aleluya!"—Mkonzi.] Kodi inu mungakachite zimenezo? ["Yesu! Zikomo Inu, Yesu!"] Ndiye kazipitani, ndipo Ambuye akhale ndi inu, ["Ulemerero ukhale kwa Mulungu! Aleluya!"]

Inu muli bwanji? Ife tiri alendo, nafenso.

82 Kodi inu mukukhulupirira? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Ndicho chizindikiro. Tsopano Liwu, likuti, "Mubwerere ku Mawu!"

Sindikukudziwani inu; Iye akukudziwani. Ngati Iye ati andiuze ine chinachake chokhudza inu, ndiye inu mukhulupirira kuti Mawu aja amene ine ndawanena atsimikiziridwa? Ndiko—ndiko kutsimikiziridwa kwa Iwo. Mukuona? Ine ndinanena kuti Iye wachita izo; kumeneko kunali kulosera. Tsopano ngati ulosi ufika pokwaniritsidwa, ndiye Iye anati, "Mumvere izo."

Inu muli ndi vuto la manjenje lalikulu limene inu mukuvutikana nalo, manjenje. Ndipo inu muli ndi chophuka, ndipo chophukacho chiri pa mwendo wanu. Ndiko kulondola, sichoncho? [Mlongo akuti, "Inde."—Mkonzi.] Tsopano kodi inu mukukhulupirira? ["Inde, bwana."] Ndiye kazipitani pa njira yanu, ndipo muzikhulupirira. Ndipo, monga inu mwakhulupirira, chomwechonso zikhale kwa inu.

83 Inu muli bwanji? Ine sindikukudziwani inu, koma Mulungu akukudziwani inu. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine mavuto anu? Tandiyang'anani ine. Inu muli ndi mavuto. Koma kwenikweni inu mwaima pano chifukwa cha winawake, ndipo ndi mmodzi amene analeledwa ndi inu. Ndi mchemwali. Ndiko kulondola. Tsopano kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine chimene chavuta ndi mchemwali wanuyo? Kodi inu muvomereza zimenezo? Iye ali ndi vuto la mtima. Ndiko kulondola. Kodi inu mukukhulupirira kuti iye achiritsidwa tsopano? Ndiye, molingana ndi chikhulupiriro chanu, zikhale choncho kwa inu.

Bwerani, dona. Inu muli bwanji? Ngati Mulungu atandiuza ine limene liri vuto lanu, kapena zimene inu mwazichita, kapena chinachake, kodi izo zikupangitsani inu kukhulupirira? Inu mukudziwa kuti ine sindi...i—i—ine sindikukudziwani inu. Limenelo lingakhale khalidwe Lake likuzizindikiritsa Lokha mwa ine, molingana ndi Mawu amene Iye anawalonjeza. [Mlongo akuti, "ine ndikhulupirira basi zimenezo."—Mkonzi.] Inu mukukhulupirira zimenezo? ["Inde. Ameni."]

Ndinu wina, inu muli ndi zovuta monga mkazi wa usinkhu wanu angakhalire nazo, koma lingaliro lanu lenileni ndi la winawakenso. Chokhumba chanu kwa Mulungu; inu mukumufunafuna Mulungu osati kwa inueni, koma kwa winawakenso, ameneyo ndi mwamuna. Ndi mwamuna wanu. Ndipo iye ali ndi vuto la mtima. Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye...Mulungu amuchiritsa Iye? Kazipitani, mukukhulupirira zimenezo. Ndipo, monga inu mwakhulupirira, chomwechonso izo zikhala kwa inu.

84 Tsopano, mukuona, kulalikira konseko, kwa ora lija limene ine ndakhala ndikulalikira. Izo, kuti zonse zimene izo zinali, anthu atatu kapena anayi adutsapo, tsopano ine ndikulephera ngakhale kuti ndiime pano. Mukuona? Mwaona, basi khamu lonseli likungowoneka mwa mkaka, kuzungulira kuno. Mukuona? Yesu anati, "Mphamvu zandichokera Ine." Ndipo ngati mkazi mmodzi, kukhudza chovala Chake, zinachotsa mphamvu kuchokera mwa Iye, ndipo Iyeyo Mwana wa Mulungu; nanga bwanji ine, wochimwa wopulumutsidwa mwa chisomo Chake?

Iye anati, "Zinthu zimene Ine ndikuzichita inunso muzidzazichita. Zochuluka kuposa izi inu muzidzazichita." Ine ndikudziwa kuti King James amati, "zazikulu." Koma ngati inu mutatenga kumasulira kwapachiyambi, anati, "Zochuluka kuposa izi inu muzidzazichita." Palibe amene angachite zazikulu. Iye anaukitsa akufa, ndipo anaimitsa chirengedwe, ndipo anachita chirichonse. Koma Iye anati, "Zochuluka zoposa izi inu muzidzazichita, chifukwa Ine ndikupita kwa Atate."

"Dziko silimadzandiwonanso Ine; koma inu muzidzandiwona Ine, pakuti Ine..." Taonani, "Ine," Ine—Ine ndi puronauni ya umwini. "Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu." Ndiye, si munthuyo. Ndi Khristu.

85 Ine ndikunena zimenezo, kuti ndizigwedeze ndekha pang'ono pokha, kuti ndikhale ngati ndazibweza ndekha. Iwe umafika pamalo mpaka kuti pakapita kanthawi...Si pamene iwe uli pamwamba apo, kapena pansa apa; ndi pakati kati. Ndi angati akumvetsa zimenezo? Ine ndikudziwa inu—inu mukuganiza kuti inu mukumvetsa. Ine ndikutero, inenso.

Kodi inu munayamba mwadziwapo kuti andakatulo ndi aneneri nthawizonse amakhala amanjenje? Ndi angati amadziwa zimenezo?

Ndi angati anawerengapo za William Cowper, wandakatulo wamkulu wa Chingerezi? Inu mukudziwa, analemba, "Pali kasupe wodzaza ndi Magazi, ochokera ku misempha ya Emmanuele." Iye atatha kulemba nyimbo imeneyo, kodi inu munamva zimene zinamuchitikira iye? Ine ndinaima pafupi ndi manda ake osati kale litali. Iye anayesera kuti achite kudzipha, ndipo anadzigwetsera mu mtsinje.

Ndi angati amene anayamba amvapo za Stephen Foster, anamupatsa Amereka nyimbo zopambana za chikhalidwe chake? Iye anali nazo izo mmutu koma osati mu mtima. Nthawi iliyonse kudzoza kukamukhudza iye, iye amakhoza kulemba nyimbo. Ndiye pamene kudzoza kwamuchokera iye, iye samadziwa kuti achite chiani ndi iyemwini, ndipo iye anataika. Iye—iye—iye anali akuledzera. Ndipo potsiriza pamene iye anayamba kuti achoke mu kudzoza kumeneko, iye anamuitana wantchito wake, ndipo anatenga lezala ndi kudzipha yekha. Izo nzoona.

86 Tayang'anani pa Eliya, mneneri. Iye anapita pamwamba apo ndipo anaitanitsa moto kuchokera kumwamba; anaitanitsa mvula kuchokera kumwamba pa tsiku loyamba; ndipo anatsekera miyamba ndipo anachita zonse izo. Ndiye pamene kudzoza kunamuchokera iye, iye anapita ku chipululu ndipo ankafuna

kuti akafe. Ndipo Mulungu anakamupezako iye, patatha masiku forte, atadzikokera mu mphanga. Sichoncho?

Tamuwonani Yona, mneneri. Atatha kupereka uthenga wake, iye anakwera pamwamba ndipo anakakhala pa phiri, anamufunsa Mulungu kuti amulole afe. U-hu. "Mulole wantchito wanu amuke mu mtendere."

Anthu samazimvetsa zimenezo. Ayi, ayi, inu simungatero. Ngakhalenso ine sindingafotokoze, ngakhale munthu winayo. Inu simungathe kumufotokoza Mulungu. Mulungu samadziwika ndi kafukufuku wa sayansi. Mulungu amadziwika ndi chikhulupiriro. Iye timamukhulupirira Iye. Inu mungazifotokoze chotani? Kodi izo zingakhale bwanji chikhulupiriro, apanso? Iye timamudziwa Mulungu mwa chikhulupiriro.

Mpingo sudzadziwa konse kuvutikira kwake ndi kulemetsa, ndi mavuto ndi mayesero, zimene zayesera kuti ziwubweretse Iwo, Uthenga. Iye amatero. Mphotho yanga siimabwera kuchokera kwa anthu.

87 Taonani apa, dona. Inde, mofulumira. Mkazi ameneyo ali ndi mthunzi waku imfa. Mulungu sakubwera kwa mkaziyo nthawi yomweyo, ine ndikukhoza kuwona...Kodi inu simukuwona mdima umene wapachikika pomuzungulira iye? Iye afa, chimodzimidzi basi monga dziko. Kuno osati kale litali, iwo anajambula chithunzi cha chinachake monga chimenecho, ndipo ndiri nacho icho kunyumba. Iye ali ndi mthunzi wakuda wapachikika pafupi ndi iye. Iye ali ndi mthunzi waku imfa.

Dona wamng'onoyo anachitidwapo oparesoni. Ndipo mu oparesoni iyi, iwo anamuchita oparesoni chifukwa cha khansara. Ndipo tsopano iye akumakhala ndi mavuto, mitundu yonse ya—ya, chabwino, zangokhala zomuchitikira zambiri. Chinthu chimodzi, ndinu wofooka kwambiri inu simukutha kuima. Chinthu china, ndi chakuti kuchokera mu chikodzodzo mukumakodza mafinya. Tsopano, kuchitira kuti inu muwone kuti ine sindikungonena chinachake. Mukuona? Ndiko kulondola kumeneko. Koma, dona, adokotala anayesera. Ine ndikumuyamikira iye chifukwa cha izo. Koma, iye anali mankhwala, koma Mulungu ndiye wochiritsa. Inu mungafe monga choncho. Iye anachita zonse zimene iye akanachita. Kodi inu mukukhulupirira? [Mlongo akuti, "Inde."] Bwerani kuno, miniti yokha.

Ndi ulamuliro wopatsidwa kwa ine ndi Mulungu Wamphamvuzonse, kuchitiridwa umboni kwa ine ndi Mngelo, amene ali pano tsopano mmawonekedwe a Lawi la Moto, ine ndikumutsutsa mdierekezi uyu amene akutenga moyo wa mkazi uyu. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Pitani, mukukhulupirira tsopano. Ndi zonse zimene ziri mwa inu, kakhulupirireni.

88 Inu muli ndi vuto limene limapha anthu ambiri kuposa china chirichonse, vuto la mtima. Iwo amazinenera kuti ndiyo nthenda nambala wani, koma si choncho, bwana. Tchimo ndilo nthenda nambala wani. Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye ndi wokhoza kuchiritsa vuto la mtima limenelo ndi kukupangani inu wabwino? [M'bale akuti, "Ine ndikudziwa kuti Iye akhoza."—Mkonzi.] Ndiye kazipitani, mukhulupirire zimenezo. Mulungu akudalitseni inu.

Inu mukuganiza kuti Mulungu akhoza kuchiritsa nsana wanuwo ndi kukupangani inu wabwino? Kodi inu mukukhulupirira izo ndi mtima wanu wonse? Muzipita, mukukhulupirira izo, mlongo. Mukawone zimene zitakachitike kwa inu, inu mukhala bwino.

Nyamakazi ndi vuto la mtima. Koma inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kukuchizani inu? [Mlongo akuti, "ine ndikutero."—Mkonzi.] Ndi mtima wanu wonse? ["Inde, bwana."] Inu muvomereza izo? ["Inde, bwana."] Monga momwe mwakhulupirira, ndi momwe ziti zikhalire kwa inu. Tsopano pitani, mukakhulupirire izo ndi mtima wanu wonse, ndipo Mulungu akuchiritsani inu.

89 Inunso muli ndi vuto la nsana. Kodi inu mukukhulupirira kuti Yesu Khristu akhoza kukuchiritsani inu? [Mlongo akuti,

"Inde, bwana."—Mkonzi.] Zipitani tsopano, mukhulupirire izo ndi mtima wanu wonse. Ine sindingathe kukuchiritsani inu, mwaona.

Kugwa, manjenje, ndipo komanso inu muli ndi nyamakazi. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kukuchizani inu, kukuchizani inu? Kodi inu mukuvomereza zimenezo? Pitani, ndipo muzikhulupirira izo, ndiye.

Zimakupangitsani inu kukhala maso nthawi zambiri, mumakhosomola. Koma Mulungu amachiza mphumu. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [M'bale akuti, "Inde, bwana."—Mkonzi.] Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye akuchiritsani inu tsopano? ["Inde, bwana."] Mulungu akudalitseni inu. Zikomo inu, chifukwa cha chikhulupiriro chanu.

Nanga bwanji ngati ine nditati ndisanene mawu kwa inu, kungoika manja anga pa inu, kodi inu mungakhulupirire? [M'bale akuti, "Inde."—Mkonzi.] Bwerani kuno. Ine ndikuika manja anga pa inu, mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo nyamakazi ikusiyeni inu. Iyo ikuchoka.

Bwerani. Bwerani, mlongo. Kodi inu mukukhulupirira? [Mlongo akuti, "Inde, bwana. Ine ndinayamba ndachiritsidwapo ndi Ambuye."—Mkonzi.] Chabwino, zimenezo ndi zodabwitsa. ["Aleluya!"] Ndiye mupite mukadye chakudya chanu cha masana, ndipo mmimba mwanu mukakhala bwino bwino. ["Aleluya! Aleluya! Aleluya!"]

Vuto la nsana lambiri, ilo lakhala likukuvutitsani inu kwa nthawi yaitali. Pitani, mukukhulupirira inu... Pitani, mukukhulupirira inu mukhala bwino, ndipo Mulungu akuchitirani inu zimenezo. [M'bale akuti, "Mulungu watero. Ameni."—Mkonzi.] Ameni. Ndizimenezotu. ["Ambuye alemekezeke."] Ambuye akudalitseni inu, m'bale. Ameni.

Matenda a shuga si kanthu, kuti Mulungu akuchiritseni. Iye akhoza kuwachiritsa iwo. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Mlongo akuti, "ine ndikutero."—Mkonzi.] Chabwino. Ndikuvomereza zimenezo, ndipo pitani mukumukhulupirira Iye tsopano ndi mtima wanu wonse.

Inunso mulinayo iyo mu magazii anu. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu? Pitani, mukakhulupirire izo ndi mtima wanu wonse, ndipo mukakhale bwino.

Inu mukukhulupirira Iye anakuchiritsani inu ndiye pamene icho chinakukhudzani inu? Iye anatero.

Vuto la uzimayi. Vuto la mtima. Inu mukukhulupirira izo? [Mlongo akuti, "Ndikukhulupirira izo."—Mkonzi.] Pitani, mu—mukachiritsidwe mu Dzina la Yesu.

90 Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu achiritsa nsana wanuwo, impsyo zanu zikhala...Akudalitseni inu! Basi kazipitiranibe.

Ine sindimachiritsa. Ine sindingathe kukuchizani. Ine si mchiritsi.

Kodi inu munaganiza chiani pamene Iye ananena za nsana wa awo, kodi inu mukukhulupirira kuti wanu wachiritsidwa, nawonso? Chabwino, ingopitani, mukukhulupirira zimenezo, ndiye...Muzingopita mukukhulupirira zimenezo, ndi mtima wanu wonse.

Wanunso, kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchiritsani inu? Pitani, mukakhulupirire izo, ndi mtima wanu wonse. Mulungu apereka izo ngati inu...Inu muyenera kuti mukhulupirire izo, mulimonse.

Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchiritsani inu, inunso? [Mlongo akuti, "Ambuye alemekezeke! Ine ndithudi ndikutero."—Mkonzi.] Chabwino. Mulungu akudalitseni inu. Muzingosunthira chamtsogolo ndi kumakhulupirira ndi mtima wanu wonse.

Bwerani, bwana. Kuwukha koyera kwakale kukuwukhira pansu. Kufufuza kwa izo kumasonyeza matenda a shuga. [M'bale akuti, "Matenda a shuga."—Mkonzi.] Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye akuchiritsani inu? Tiyeni tipite ku Gologota kuti mukapatsidwe magazii tsopano. Mwa chikhulupiriro, mu Dzina la Yesu Khristu, mulole iye achiritsidwe. Ameni. Mulungu akudalitseni inu, m'bale. Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Kodi inu mukukhulupirira? ["Kulondola ndendende."]

91 Nanga bwanji ena a inu mwa omvetsera tsopano? Kodi inu mukukhulupirira ndi mitima yanu yonse, kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse? Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.]

Nanga bwanji chigawo ichi? Dona wamng'ono amene wakhala, akuyang'ana kumene pa ine pamenepo, akuvutika ndi vuto la uzimayi, kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu? Wavala chikhoto chaching'ono cha buluu. Chabwino. Mukhulupirire tsopano, Yesu Khristu akuchizani inu. Ndi zophweka chomwecho basi.

Dona wakhala kumbuyo kwa inuyo, watsitsi lakuda. Iye anati, "Zikomo Inu, Ambuye." Chinachake chamukhudza iye. Iye samadziwa kuti Icho chinali chiani. Vuto la chikodzodzo lakusiyani inu, atakhala pomwepo, kumbuyo komwe kwa dona yemwe anachiritsidwa pomwe apo. Ngati inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse pamenepoyo, dona.

Inu mukutero? Chabwino, kwezani mmwamba dzanja lanu ngati inu mukufuna kuti muvomereze zimenezo. Mulungu akuchizani inu.

Nanga bwanji uyu pansu apa, winawake umu?

92 Kumbuyo uko mwa omvetsera, tsopano mukhale molemekeza kwenikweni. Musasunthe. Mukuona, matenda awa amapita kuchoka pa wina kupita pa wina.

Nanga bwanji inu, bwana? Bambo wokalamba uyu amene wakhala apa mu mpando uwu? Kodi inu mukukhulupirira? Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kukuchizani inu? Nyamakazi, ndipo inu muli ndi kubanika. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu achiritsa zimenezo? Inu mukutero? Chabwino, inu mukhoza kulandira zimene inu mwazipempha. "Ngati inu mungakhulupirire!"

Kodi inu mukuganiza chiani, dona, mwakhala pafupi ndi iyeyo? Kodi inu mukukhulupirira, inunso? Kodi inu mukukhulupirira? Kodi inu mukukhulupirira Mulungu akhoza kundiuza ine kuti vuto lanu ndi chiani? Inu muli kutali ndi ine. Mungomukhulupirira Iye tsopano. Kodi inu mukukhulupirira kuti ine ndakuuzani inu Choonadi? Ndiye kukwera kwa magazi kwanu kutsikira pansi. Inu mukukhulupirira zimenezo?

Inu munakwezera mmwamba dzanja lanu, inunso. Inu mumayesera kuti mumulimbikitse iye. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine zimene...Inu mwakhala wabwino kwambiri kuti mumuthandizire iye, tsopano Mulungu akhala wabwino kuti akuthandizeni inu. Inu muli ndi vuto lauzimu limene lakhala likukuvutitsani inu. Ngati zimenezo ndi zoono, mugwedeze dzanja lanu monga chonchi. Izo zikonzedwa tsopano. Iye wakonza zimenezo.

93 Ndi angati akukhulupirira? Ndi angati a inu ati avo-... ameneyo si Mkhristu, ali ndi—kumverera kwakuti Yesu Khristu ali pompano, amene akufuna kuti aimirire tsopano, ndikuti, “Yesu, ine ndikufuna kuti ndizizindikiritse ndekha ngati wochimwa, kodi Inu mundikhululukira ine machimo anga?” Muimirire pa mapazi anu. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Ndizo...Mulungu akudalitseni inu, inu, inu, inu. Ichi, Iye akukuwonani inu. Iye amalemba dzina lanu pamene inu muchita zimenezo.

Cha kuno ku chipinda chammwamba, imirirani, ndikuti, “Ambuye Yesu, ine ndikufuna kutero, ine ndikufuna kuti ndizindikiritse. Ine ndikufuna chifundo chifukwa cha moyo wanga.” Mulungu akudalitseni inu, bwana. “Ine ndikufuna chifundo, Ambuye Yesu.”

Iwe sukutha kuwona, mzanga, ndi Iyeyo pano? Mulungu akudalitse iwe, mnyamata. Mulungu akudalitse iwe. Mulungu akudalitse iwe, dona wamng'ono. Ndicho chinthu chopambana chimene iwe unayamba wachichitapo. Tsopano winawakenso amene sanachite chimenecho, imirirani, ndikuti, “ine ndikufuna kuti ndizindikiritse, Ambuye Yesu. Ine ndikuzizindikiritse ndekha, usikuuno.”

“Iye amene adzavomereze tchimo lake, adzapeza chifundo. Iye amene abisa tchimo lake, sadzachita bwino.”

Kodi inu mutero, mu Kukhalapo Kwake? Mulungu akudalitseni inu, dona. Ine ndikufuna...Mulungu akudalitseni inu. Inde. Ndipo Ambuye akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu, dona. Ambuye akudalitseni inu.

Inu mukuti, “Kodi zimenezo zikutanthauza chirichonse?” Pakati pa imfa ndi moyo, ndiko kusiyana kwake.

Kodi inu mukuzindikira Kukhalapo Kwake pano? Kodi inu mukukuzindikira iko? Kodi inu mukumverera zimenezo? Mukuona, inu mukuziona Izo, inu mukuziwona Izo zikugwira ntchito. Ndi Iyeyo. Ndizo ndendende zimene Iye ananena kuti Iye akanadzachita. Kodi inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

94 Winawakenso akuti, “Ine ndikufuna kuti ndizizindikiritse ndekha ngati wochimwa, Ambuye. Inu mundikhululukire ine machimo anga tsopano.” Ngati inu mwaima kale, mungokwezera mmwamba dzanja lanu. Ena a inu mwazungulira makoma, kwezani...Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Wina wakenso akuti, uko mu chipinda chammwamba mmbuyo, mukuti, “Ine ndikufuna kuti ndizizindikiritse ndekha, Ambuye Yesu. Ine ndikupempha chifundo, usikuuno, mu Kukhalapo Kwanu Kwaumulungu, ndikukhulupirira kuti, Mulungu kumene amene ati adzandiweruze ine, Kukhalapo Kwake kuli pano tsopano. Iye akudziwa kuti Iye akulankhula kwa mtima wanga ndipo akundiiza ine kuti ndikulakwitsa. Ine ndikufuna kuti ndiimirire ndikuti ine ndine wolakwa. Ine ndikuvomereza cholakwitsa changa. Inu mukunditsutsa ine, mu mtima mwanga.” Ndicho chifukwa ine ndinamitsa mzere wa pemphero. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu.

Kodi inu mukuganiza kuti ine ndinawuyimitsiranji iwo? Ine ndinawuyimitsa iwo chifukwa ine ndinadziwa kuti zimenezo zichitika.

Tsopano, alipo ena pano, kodi inu simuimirira? Imirirani ndikuti Chinachake chikulankhula kwa mtima wanu, inu mukulakwitsa. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. “Ndine wolakwa. Mundikhululukire ine, Ambuye. Ine ndikuzizindikiritse ndekha. Ine ndaimirira, Ambuye, Pamaso Panu. Ine ndikudziwa kuti Inu muli pano. Ine...Inu muyenera kukhala muli pano. Inu munanena kuti ichi chidzakhala—chinthu chimene Inu mukanadzachita. Tsopano ine...ine ndikuwona chizindikiro, ndipo ine ndikudziwa kuti izo zafotokozedwa kwa ine kuti icho chiyenera kukhala chizindikiro cha tsiku la lero. Ine ndikumva Liwu limene linaitana kuti ndibwerere ku kulapa. Ndine pano, Ambuye. Ine ndikukhulupirira chizindikiro. Ine ndikumva Liwu.”

95 Liwu likulankhula ndi inu tsopano! Bwererani, O omwazika! Bwererani, O nyenyezi yoyendayenda! Bwererani, O inu amene mwaponyedwera kunjala! Bwererani, usikuuno!

Kodi inu simubwerera? Ingoimirirani ndikuti, “ine ndikuzizindikiritse ndekha ngati wochimwa,

ndikupempha chifundo.” Kodi inu muchita zimenezo, wina wakenso? Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitse iwe, pamwamba apo, mwana. Ngati ine ndingakuphonyeni inu, Iye sangatero. Mulungu akudalitseni inu, dona. Zimenezo ndi zabwino kwambiri. Zimenezo ndi zabwino kwambiri. Wina wakenso? Ingokhalani...Ine ndikufuna kuti ndidikirebe kanthawi pang'ono, chifukwa ine ndikumvererabe kulemedwa pano, mwaona. Wina wakenso? Mulungu akudalitseni inu, dona. Ndi momwe muyenera kuchitira izo. Ndi zimenezotu. Wina wakenso, “Ine ndikufuna kuti ndizizindikiritse ndekha, ndingoimirira ndekha ndikuti ndine wolakwa. Ine ndikupempha chifundo”? Kodi inu muchita izo? Mofulumira ndithu ife tisanapite patsogolo, dzukani ndikuti, “ine ndikufuna kuti ndizizindikiritse ndekha, Ambuye Yesu.” Mulungu akudalitseni inu, dona wamng'ono.

96 Inu mukudziwa, mwinamwake inu musanakafike kwanu, koma nthawizina kapena imzake padzakhala chifunga chozizira chidzabwere pa nkhope yanu. Mwinamwake mmawa wina adokotala adzabwera ndipo adzamverera kugunda kwa mtima wanu kukukweza mpaka mnkhwapa, palibe chimene chingathe kuchitidwa. Ndiye inu mudzamverera mafunde ozizira a imfa akuyandama pa nkhope yanu. Inu mudzakumbukira zimene inu mwazichita.

Kumbukirani, iwo sangakukwirireni inu mwakuya kwambiri, iwo sangathe kuchita kalikonse kwa inu. Mulungu analonjeza, “Ine ndidzakuukitsani inu kachiwiri, pa tsiku lomaliza.” Taonani. “Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya ndipo sadzabwera ku Chiweruzo, koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.” Winawake afufute Zimenezo ngati inu mungathe. Yesu Khristu ananena Zimenezo. “Iye amene akhulupirira, ndiye kuti, amene amvetisa Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya, sadzabwera konse ku Chiweruzo, kutsutsidwa, koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.” Chifukwa, iye wakhulupirira pa Mwana wobadwa yekhayo wa Mulungu, amene Mulungu anamuukitsa, zaka zikwi ziwiri zapitazo, ndipo ali wamoyo pano, usikuuno, akusonyeza maganizo Ake a chiukitsiro Chake.

97 Kodi pangakhale wina amene angaimirire, zitatha zimenezo, ena akuti, “Ine ndikufuna kuti ndiwalandire Iwo. Ine ndikufuna kuti ndimulandire Iye.” Mulungu akudalitseni. Mulungu akudalitseni inu. Zimenezo ndi zabwino kwambiri, dona wamng'ono. Chimenecho ndi chinthu chapamwamba. Ine ndikufuna kuti inu muzindikire.

Ine ndinawona kuitanira paguwa, kuno nthawi ina kale, anthu akubwera, akutafuna chingamu, akugundana wina ndi mzake mmbali.

Koma kodi inu munazindikira kuwona mtima pa nkhope za anthu amenewo? Akazi aang'ono amenewo, ngakhale nditatha kuwadzudzula iwo za kudula tsitsi lawo, atazipentapenta; ndi kuzipentapenta kumeneko, ndi tsitsi lodula, anangoimirira chimodzimodzi basi, “Ndine wochimwa. Mundichitire ine chifundo, Mulungu.” Ndi Mbewu imeneyo ili mmenemo. Kuwala kunawalira pa iyo, ndipo iwo akudziwa zimenezo. Mulungu akudalitseni inu.

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu tsopano.

Ine ndikufuna wokhulupirira aliyense muno, amene waima pafupi ndi munthu ameneyo amene waimirira, aike dzanja lake pa munthu ameneyo, (mutero inu?), mmodzi yemwe anaimirira. Iwo anaimirira pafupi ndi inu. Ngati ndinu Mkristu, muike dzanja lanu, pa mlongo, m'bale, “Ine ndaika dzanja langa pa inu tsopano. Ine ndipempha.”

98 Atate Akumwamba, alipo pano usikuuno amene—amene akukhulupirirani Inu. “Mbewu zina zinagwera mmphepete mwa njira,” Inu munati, “mbalame zinabwerapo ndipo zinadzatola izo. Zina zinagwera pa nthaka ya miyala, ndipo minga ndi nthula. Koma zina zinapita mpaka pa nthaka yabwino, yachonde.” Ndipo Kukhalapo Kwanu popeza kuli pano, usikuuno, zawakhutitsa ambiri pano usikuuno kuti Inu ndinu Mwana wa Mulungu, kuti Ndinu wamoyo kwanthawizonse. Ndipo Inu munalonjeza, chifukwa Inu muli moyo, nafenso tikhoza kukhala amoyo.

Ambuye Yesu, iwo anakweza mmwamba ndipo anaimirira ngati mboni kuti iwo akukhulupirirani Inu. Tsopano, Ambuye, ine ndikudziwa kuti Inu mudzawaimira iwo pa Tsiku limenelo. Perekani izi, Ambuye. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu. Mulole iwo azikapita ku mpingo wina wabwino ndipo akabatizidwe mu ubatizo wa Chikristu. Mulole iwo akadziphatike okha ndi gulu lina labwino la okhulupirira. Mulole iwo akadzazidwe ndi Mzimu Woyera. Mulole iwo adzakhale zikho za Uthenga, ngale mu korona Wanu pa Tsiku limenelo. Ndipo ngati ine sindidzawawonanso iwo kachiwiri mbali ino ya Tsiku lalikulu limenelo, mulole ine ndidzawawone iwo pa Tsiku limenelo monga zinali mmasomphenya, akuti, “Kodi inu simukundikumbukira ine? Kunali ku Baton Rouge, usiku uja, pamene ine ndinaimirira.” Perekani izi, Atate. Iwowo ndi Anu, kudzera mu Dzina la Khristu.

99 Apa pali, patsogolo panga, bokosi la mipango, nsapato zing'onozing'ono, tinsapato ta ana, mipango, ndi nsaru, ndi zovala. Ife timaphunzitsidwa, mu Baibulo, kuti iwo anatenga kuchokera mthupi la Paulo Woyera, mipango ndi zovala, mizimu yosayera inawachokera anthuwo. Tsopano, Atate, ife tikudziwa kuti sindife Paulo Woyera, koma Inu mukadali Mulungu yemweyo, kotero ine ndikupempha kuti Inu mupereke

zotsatira zomwezo, pamene moona mtima kambadwo kano kakukhulupirira. Iwo sanamukhulupirire Paulo chifukwa iye anali Paulo; anamukhulupirira Paulo chifukwa Inu munazizindikiritsa Inunokha ndi Paulo. Tsopano iwo akukhulupirira chinthu chomwecho usikuuno, Ambuye, kuti Inu mwazindikiritsidwa pakati pathu, usikuuno. Ndipo tsiku lina, ife tidzanena kuti...

Wolemba wina amatiuza ife, kuti, "Israeli anali pa njira akupita ku dziko lolonjzedwa, ndipo Nyanya Yofiira inawatekereza, kuwalekanitsa iwo ndi dziko lolonjzedwa." Wolemba ananena, kuti, "Mulungu anayang'ana pansu kudzera mu Lawi la Moto lija, ndi maso awukali, pamene Ilo linkayenda pa a Israeli. Ilo linkachititsa khungu, mdima kwa osakhulupirira, ndi kuwala kwa Israeli. Ndipo pamene Nyanja Yofiira iyo inawatekereza iwo, iyo inachita mantha, ndipo iyo inadziyalulira mmbuyo, ndipo Israeli anawoloka kumapita ku dziko lolonjzedwa pa nthaka yowuma."

Ambuye Mulungu, muyang'ane pansu usikuuno, kudzera mMagazi a Yesu Khristu, Mwana Wanu. Pamene ine ndikuyika manja anga pa mipango iyi; pamene iyo ikaikidwe pa odwala, mukalole Mzimu Woyera, Ambuye, ukayang'ane pa munthu ameneyo, ndipo mulole matenda akachoke pa iwo, ndipo iwo akawolokere kupita ku dziko lija la thanzi labwino ndi mphamvu. Pakuti, Baibulo linati, "Pamwamba pa zinthu zonse," kuti iwo ankakhumba kuti "tidzakhale a thanzi labwino." Perekani izi, Ambuye. Ine ndikuwatumiza iwo, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

...ine ndidzamsatira,

Komwe Iye anditsogolera...(tiyeni tingoimba)

...ndidzamsatira,

Ndinka Naye, (tsopano Kukhalapo Kwake kuli pano, tiyeni tizingompembedza Iye mu nyimbo, mokoma), njira yonse.

100 Mungathe kuyiimba iyo kwenikweni monga chonchi? Komwe Iye anditsogolera,

Komwe Iye anditsogolera, Komwe Iye anditsogolera,

Ndinka Naye, (ngati inu mungathe, tsopano kwezani mmwamba manja anu), Naye njira yonse.

Tiyeni ife tiimirire tsopano, mukweze manja anu kachiwiri.

...Naye mpaka mmundamo,

Aliyense ayimbe mu Mzimu tsopano. Uthenga wocheke kwenikweni. Tiyeni timupembedze Iye mu Kukhalapo Kwake. Iye amakonda kuti azipembedzedwa.

...mmundawo,

Ndinka Naye mpaka mmundamo, Ndinka Naye, Naye njira yonseyo.

Tsopano tiyeni tizing'ung'uza iyo. "Ine ndikhoza..." Tsopano pamene inu mukuchita zimenezo, ine ndikufuna kuti inu mugwirane chanza ndi winawake, ndikuti, "Mulungu akudalitseni inu, mwendamnjira. Mulungu akudalitseni inu, mwendamnjira," monga choncho. Ndife mmodzi ndi wina ndi mzake. Amethodisti, ndi Abaptisti, Apresbateria, Achipentekoste, tonse tigwirane chanza wina ndi mzake. "Mulungu akudalitseni inu, mwendamnjira." Ndicho chimene ife tiri: amwendamnjira.

...mmunda,

Mulungu akudalitseni inu, mwendamnjira. Mulungu akudalitseni inu. [M'bale Branham ndi osonkhana akupitirira kugwirana chanza. Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

...mmunda,

Tsopano tiyeni tikweze manja athu.

Ndinka Naye, ndi Iye njira yonse.

101 Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu, modzichepetsa, mu pemphero. Musaiwale, mmawa, Sande sukulu.

Mwanjira ina kapena imzake, ine ndikungomverera Kukhalapo kwa Mulungu kwenikweni mu mtima mwanga. Zikukhala zondivuta kwambiri kuti ine ndichokepo, usikuuno, mwanjira ina. Ine ndikumverera kuti Mzimu Woyera wakondweretsedwa, usikuuno. Ife mwinamwake tikhala ndi msonkhano wawukulu mawa, kuwawona anthu akubwera kwa Khristu, inu mukuona. Winawake akudabwa chifukwa chimene ine sindinapangire kuitanira paguwa. Ine ndidikirira mpaka nditatsogozedwa kuti ndipange zimenezo. Mukuona?

Ine ndikudalira kuti aliyense amene anakweza dzanja, kapena anaimirira, ine ndikudalira kuti mawa

mukakhala pa mpingo wina wabwino, kukatenga malo anu pakati pa okhulupirira.

Pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, tiwapempha abusa pano kuti abwere patsogolo, ngati iwo angathe, kuti atibalalitse. Mulungu akudalitseni inu tsopano, ndi mitu yathu ndi mitima yoweramitsidwa pamaso pa Mulungu.



www.messagehub.info

Maulaliki wolalikedawa ndi
William Marrion Branham
"...mu masiku a liwu..." Chivumbulutso 10:7